# MVETSA 2

V J Kafantenganji

KKF

Chewa ZM5724CP

# MVETSA 2

V J Kafantenganji

Kenneth Kaunda Foundation

© Kafantenganji 1986

First Published 1986 by
Kenneth Kaunda Foundation
(Publishing and Printing Division)
P.O. Box 32664, Lusaka, Zambia

Printed in Zambia by Kenneth Kaunda Foundation
(Publishing and Printing Division)

PL
8110
.C5
K34
1986
v. 2

# ZA M'KATIMU


| *Phunziro* | | *Tsamba* |
|---|---|---|
| | Mau Oyambirira | v |
| 1. | Manyazi Apweteketsa | 1 |
| 2. | Kwathu | 6 |
| 3. | Nsanje | 11 |
| 4. | Mwai Ndi Tsoka | 17 |
| 5. | Coipa Citsata Mwini | 23 |
| 6. | Kuluzi | 29 |
| 7. | Mawa | 38 |
| 8. | Maina | 45 |
| 9. | Mphatso | 52 |
| 10. | Tchopa | 59 |
| 11. | Ndiwo | 64 |
| 12. | Kudzida | 71 |
| 13. | Zakumwa Za aMalawi 1 | 80 |
| 14. | Dzimbu | 85 |
| 15. | Panchepera Zanchepera | 90 |
| 16. | Zakumwa Za aMalawi 2 | 97 |
| 17. | Zamtsogolo | 101 |
| 18. | Imfa Sithawika | 107 |
| 19. | Zakumwa Za aMalawi 3 | 115 |
| 20. | Cuma | 119 |
| 21. | Kupha Kambuku 2 | 126 |
| 22. | Cipongozi 1 | 129 |
| 23. | Kusaka 2 | 132 |
| 24. | Umasiye 2 | 136 |
| 25. | Kudzikonda 2 | 139 |
| 26. | Cokolo 2 | 142 |
| 27. | Mankhwala 2 | 146 |

28. Kuphunzirana 2 ..... 151
29. Cipongozi 2 ..... 155
30. Kufanana kwa Mitundu 2 ..... 159
31. Mwana Ndinkhoswe ..... 163
32. Mankhwala 3 ..... 166
33. Kupha Kambuku 3 ..... 170
34. Mitala 2 ..... 173
35. Kulimba Mtima 3 ..... 177
36. Kusiyana Kwa Anthu 2 ..... 181
37. Kufanana Kwa Mitundu 3 ..... 185
38. Nchito ..... 190
39. Mphulumukwa ..... 194
40. Nomi ..... 200
Mau Ndi Matanthauzo Ake ..... 206

..... 151
..... 155
..... 159
..... 163
..... 166
..... 170
..... 173
..... 177
..... 181
..... 185
..... 190
..... 194
..... 200
.....206

## MAU OYAMBIRIRA

Mvetsa 2 ndi buku lotsiriza la mabuku awiri a Mvetsa. Colinga ndi malembedwe, lifanana ndi buku loyamba: Kuphunzira mau, matanthauzo monga akhalira pa nthawi zosiyana-siyana ndiponso machulidwe ake.

Ndayesa kuikamo zina zambiri zimene mulibe m'buku 1. Zambiri ndizocititsa cidwi ndi zopatsa phamphu anthu wodziwa m'magonero a Cichewa kuti afukule zambiri za cilankhulidweci. Ine ndine kashole, woshosha maganizo a anthu anzeru kuti apeze zinthu zofunika.

Ndipo ngati pali pena wodziwa aganiza kuti mlembi walakwa, mlembi ali wokonzeka kutsata zofuna za anthu.

V J Kafantenganji.

## PHUNZIRO 1

### MANYAZI APWETEKETSA.

Kale-kale anthu akali ocepa m'boma limene atsamunda amalicha Mwalimba, limene likulu lake linali paphiri la Ngala m'mphepete mwa mtsinje wa Buwa, munali zipululu zosaneneka. Kuyenderana pakati pa anthu, kunali kwa kataya moyo cifukwa zirombo zolusa zinali zambiri m'zipululuzo. Ndipo kujiwa kwa anthu sikunali kwa cirendo. Nthawi imeneyi nkuti ku bomali kutabwera mzungu m'modzi Bwana Green odzagwira nchito ya boma. Ndipo malinga ndi makhalidwe akale, mzunguyo anali kuopsya anthu. Anthu samadziwa kuti ndi munthu mnzawo, koma maopedwe ake, ankamuopa ngati mkango.

Nyengo ya mondokwa, midzi yozungulira mapiri a Mchiye, Pumphunthe, Lunguzi ndi Mtuwasompho, inagwedezeka ndi mbiri ya mikango yolusa. Mikangoyi inali kudya anthu ku minda pokathyola mondokwa kapena pokumba mtedza ku zirere. Ndipo kobisala kwawo kwa mikangoyo kunali kumapiri amenewa. Tsiku lina mkango unagwira mkazi wina ku Nango. Amuna atamva, anasonkhana nayamba kuutsatira kuti alanditse mkaziyo. Atayenda pang'ono, anamva mkango nuphwanya mafupa a munthuyo. Anthu anaimba makweru kuopsyeza ciromboco ndiponso kuti asamve mau a mkango utabangula. Tsono mkango utamva makweru, unadzuma. Anthu anasendera ndithu pafupi.

Ndipo anauona mkango uli pathanthwe nudya mkaziyo. Nawonso mkango utapenya gulu la anthu, unautsa cenjerere, ndi kupalasula miyendo ndipo nuopsyeza modzuma. Ataona izi anthu, anathawa napita ukagwera-na cifukwa ca mantha. Anaima panjira kupangana coti acite. Sanafune kukauputanso mkango uja. Komanso anacita manyazi kupita kumudzi. Amaopa akazi kuwatukwana cifukwa cosalimba mtima kwawo. Ndipo wina anati, nkosatheka kuupha mkango ndi zida anali nazo, ndipo anawakumbutsa kuti mzungu ndiye akhoza kuupha cifukwa ali ndi mfuti. Anzake anabvomera. Ndipo osakhalitsa anatuma mfumu kukauza mzungu kuti adzawaphere mkango.

Mzungu atamva, anacita mantha koma sanafune kuonetsera kwa mfumu ija mantha ake. Kuopa kunje-njemeretsa pakamwa, anangogunchula mutu. Analola cifukwa ca manyazi. Pokhala mzungu ndipo woopsya, kukana kukadakhala kutaya ulemu wonse amampa-tsa anthu. Anaitana msirikali wake amene anthu ankamucha Nkhondoyacepa. Ndipo mokhokhoteka anatsata pamsana pa mfumu. Maganizo anali khumi mumtima mwake. Anapita ndi mtima wodzionetsera kuti ndi wolimba mtima. Anafika mbwe!

Kufika kwake kunalimbikitsa mitima ya anthu wonse. Zokamba ndi maonekedwe a nkhope za anthu zinasonyeza cikhulupiriro cathunthu mwa mzungu uja. Ndipo wina anauza anzake kuti zirombo zikumana. Nanga akadatani namtamanda anthu? Acotse ulemu wake pokana kupha mkangowo cifukwa ca mantha? Sakatero, cifukwa akadacita mantha, anthu sakadakhu-lupirira kuti mzungu ngoopsya. Ndipo sakadacitira mwina koma kulola.

Mzungu uja anatsagana ndi gulu la anthu limene linali

ndi cikhulupiriro mwa iye. Wonse anayenda cinunu. Cinunu mwa gulu lija cinali pawiri: Kwa mzungu cimasonyeza mantha, koma kwa anthu cinali ciyembekezo ca cipulumutso. Anafika, onse anaima jega! 'Uli kuti?' anafunsa mzungu ndi mau onjenjemera. Ena anamulozera pamene unagona. Anthu anaima kutali kumbuyo. Ndipo iye ali nje, nje, nje anapita patsogolo ndi msirikali wake. Pofuna kudzionetsera, anaika cipolopolo m'cikuni cautsi cake, nasanjika pa phampha la msirikali wake ndipo iye nakhala kumbuyo kwa msirikaliyo. Anacita conco cifukwa ca mantha ndi mkango. Cina nkuti mfuti zakale zinali zolemera ndipo cifukwa cacikulu, anati asandutse nyambo ya mkango msirikali wake. Anafunsa wina kuti aupute ndi mwala poulasa. Ndipo anaponyadi. Uliponi balamanthu! poyera. Unali kuzaza, utautsa cenjerere, maso ali tunzu! ndipo mano ali mbee! pamtunda. Mzungu thupi linadzala madzi. Ndipo mosaupenda, anaomba cikuni cautsi cija. Wauputa mkango. Unalumpha lee lee lee kulunjika mzungu wamaso anai uja. Mzungu poti afutuke, msirikali anathawira pambali ndipo poti aponye mwendo wina kumbuyo kuti aime bwino, mwendo umodzi unalowa m'dzenje la cizombwe. Ndipo ndi mau omvetsa cisoni akuimfa analira mai wake ngati mwana. Anagwa cagada. Mwendo umodzi uli pholi! kumwamba. Tsono cirombo cinadzabvumata ndikuphwanya nchafu yake. Popenya izi msirikali, anaika msanga-msanga cipolopolo m'mfuti yake naombera cirombo cija. Ndipo cinagwa kuti khu! kufa nkukhala komweko. Nkhondoyacepa sanaphe mkangowo cifukwa colimba mtima ai, koma anali ndi mtima woti akanena ciani ku boma mzungu akafera m'manja mwake. Cina

cifukwa ncakuti wolembedwa nchito sayenera kuthawa kusiya bwana wake nafa.

Tsono utafa mkango, anthu anabwerera kumene anathawira ndipo mothandizana ananyamula mzungu wolumidwayo pa machira ndipo ena anapika mkango. Mzungu analanguluka ali ku boma namverera kuwawa mabala ake.

## KUMVETSA NKHANI

1. Kodi boma limeneri muganiza ndi liti?
2. Kodi nciani m'masiku amenewo cinali cosadabwitsa? Nanga ndi mau oti asonyeza?
3. Cinagwedeza mitima ya anthu nciani?
4. Perekani zifukwa ziwiri anthu ankayimbira makweru polimbana ndi mkango.
5. Kodi mzungu uja anapita ndi mtima wotani?
6. Nenani zinthu zitatu zosonyeza kuti mzungu anali ndi mantha?
7. Kodi m'zocita za mzungu uja muonamo khalidwe lotani?

## KUPHUNZIRA CILANKHULIDWE

1. Phunzirani mau awa ndipo muwagwiritse nchito m'ziganizo zanu zoyenera: Maso tunzu! maso psyu! lee lee lee! balamanthu! pholi! khu! fwaa!

## MWAMBI

2. Khwangwala wamantha anafa ndi ukalamba.

## ZOKAMBIRANA

3. Munthu amalanguluka pa:-
   (i) Akafulumira kucita cinthu.
   (ii) Akacedwetsa kucita cinthu.
   Perekani zitsànzo pa mitu iyi.

## PHUNZIRO 2

### KWATHU

Kwawo kwa munthu ndi malo kumene akhala. Malo wosapukwitsa. Munthu atakhala ku malo ena, malinga ndi nthawi ndi nyengo zitapitapo ndithu, amadandaula kuti ndakumbuka kwathu. Kwathu kumene anena ndi pacisa pake. Pamalo obadwira kapena okhalapo ndi makolo ake, ndipo akhala wokondwa atafera pomwepo. Malo angaipe atani ngati munthu anazolowerapo, safuna kucokapo. Ndipo ngati wina afuna kumugwenza-gwenza, amadandaula. Palibe kanthu ndipouma, pamiyala, posowa madzi, safuna kusintha malo cifukwa n'pake ndipo ngati pali zobvuta, zimenezo makolo ake akhala nabvutika nazo kwa iye ncabe cifukwa zinamgwira thupi. Pangakhale nyumba imodzi, mwini wake anena ndithu kuti kwathu. Inde, munthu akhoza kunena kuti kwathu nku Zambia. Nzoonadi. Nanga ku Zambia kwake ndi mbali yiti? Atha kuyankha kuti ndi ku zambwe kwa Zambia. Boma liti? Ndipo mudzi uti? Yankho lomaliza ndilo liyankha kwawo kweni-kweni kwa munthu. Wina akhoza kufunsa cifukwa ninji wakuti wakuti apezeka kuti kwawo ndi malo akuti akuti? Ndipo pofuna kusanthula mpaka pamcira za m'mene anakhalira kumeneko, atha kupezeka mwina mwanjira zitatu.

Munthu amapeza malo mocita kupempha kwa mnzake. Ndipo kale mapemphedwe ake anali kuyendetsa motere. Munthu wina amakhumbira mtunda umene unali m'manja mwa mfumu ina. Mwina sikumatheka

kuti akafunse za malo aja ngati sanatsimikize cifukwa cocokera pamalo anali kukhala kale paja. Tsono zocoketsa anthu pamalo nzankhani. Cidani pamudzi, cogwera m'nkhani za ndeu, mirandu kapena ufiti, zimadzetsa cipasu-pasu. Koma ena maka acikumbe, wozolowera kupinda msana nkumasandutsa nthaka ndalama, amafuna malo wosusunuka, malo oti alimepo mwacifuniro cake conse. Kulima kopanda mkangano ndi mnzake cifukwa ca malire.

Ndipo cifukwa cocokera citapezeka, munthu wofuna malo amapita kwa mwini mtunda modzicepetsa. Ayenera kutero cifukwa galu sautsa mcira kucirendo, kwake nkupsyatira. Atakambirana koyamba, mwini mtunda amamuuza munthuyo tsiku loti adzabwerenso. Pobweranso, amafuna kuti abwere ndi wina wodzakhala mboni yake. Ndipo nayenso mwini mtunda, amakhala nafunsira-funsira za khalidwe la munthu uja. Cina, amakamba ndi anansi ake kuti asadabwe ngati munthu wina akuswa mphanje pena pake m'dziko lawo. Mwina mtunda amacita zonsezi cifukwa samafuna wakudza wamnjunju, womveka za ufiti ndi wodzitukumula. Samafuna mlendo wodzakhalitsa m'phanthi ngati nsikidzi eni mtunda. Sankafuna zimenezo. Ncifukwa cake akulu akale amati, pocoka pamsasa usamaipitsa. Amati pocoka pamalo, munthu azibvala nthenga yoyera. Tsono mlendo uja atadzanso ndi mboni yake, ndipo mbiri zake zitakhala zokoma, amamubvomera ndi kumlandira ndi manja awiri. Koma ngati ndi kabvuwebvuwe, amamkana dzuwa liwamba mtengo. Akamlola, amamfunsa ndi mbali yiti ya mtundawo anaikonda. Atanena, mwini mtunda amamdulira mtundawo. Tsono podzayamba masasa, wopemphayo amapereka camtunda, cimene nthawi zambiri mwini mtunda samanena kuti apereke ciani. Ici cimakhala kadziwa mwini mkhuto wa fulu.

Caciwiri, kwawo kwa munthu kumapezeka kwakuti kwakuti cifukwa mwina kalelo makolo ake anapeza malowo cifukwa ca mlandu. Mlandu wake wokhudza imfa ya munthu. Mwacitsanzo, mlendo wapempha malo, amlola ndipo nakhazikika. Pamudzi pamlendo pasamba mbeta ndipo mwini mtunda akhumbira, nafunsa mbeta, natenga, nakhala naye kwawo. Zaka zitapitapo ndithu, cimango ciri pacimake, mtengwa afundidwa m'thupi ndipo asanakanene kwawo, mtengwa ati nagona pano. Mudzi wonse kakasi! akanena bwanji kwawo kwa mkazi? Ndipo ndi mtima wakuti mlandu sukugwa pamtengo, amakanena maliro aja. Malinga ndi mwambo, pamakhala mlandu wothetsa malobvu mkamwa akulu a pamudzi. Pokamba mlandu nthawi yotsiriza, mwini mbumba amatsinira thako kuti adyerapo pambumba yake. Ndipo ngati amalifuna nkale dziko, imfa yambumba yake ija, imaliza ng'oma yowamba-wamba. Amakana dipo lina lirilonse, nafuna amdulireko mbali yina ya mtunda anakhalapo uja. Colinga cake amafuna malo ake akule.

Cacitatu, malo ena amapezeka cifukwa ca nkhondo. Ici cimatheka ndi mtundu wa anthu, osati munthu m'modzi ai. Kumatheka kuti kumene kuli mtundu wamphamvu wakuti wakuti, limakhala dziko losauka. Dziko louma, lamiyala ndi njala yosatha. Tsono poona malo ena kumene kuli mtundu wofoka, kwa conde, zakudya zosasowa ndipo anthu ake wopantha bwino, amasirira nafuna kulanda. Ndipo atatsimikiza kulanda malowo, ankamema nkhondo. Nkhondo imayambika mopanda cifukwa ceni-ceni. Imakhala nkhondo yankhanza ndipo ambiri amaphedwa. Tsono nkhondo itakamuka, wofuna dziko aja, samabwereranso kwawo ai. Amakhazikika m'malo osiyana-siyana m'mene amadziwa kuti ndimonona. Eni ake amawaika kumcenga wa nkhululu. Izi nzifukwa zina akuti akuti apezeka nati kwathu ndi kwakuti kwakuti.

## KUMVETSA NKHANI

1. Kodi kwawo kwa munthu kusiyana bwanji ndi malo wokhalako cabe?
2. Bwanji munthu safuna kucoka pamalo amakolo ake?
3. Kodi munthu atapempha malo, asanamulole amafunsira kumene anacoka cifukwa ninji?
4. Atakhazikika, amathokoza bwanji kwa mwini mtunda?
5. Mapezedwe a malo aciwiri anali wotani?
6. Fotokozani ubwino wake ndi kuipa kwake kwa funso lacisanu.
7. Kale mtundu wofoka umasauka polandidwa zinthu zawo. Perekani zitsanzo munamva kapena kuwerenga za mapezedwe a malo ali m'ndime yotsiriza ya nkhaniyi.

## KUPHUNZIRA CILANKHULIDWE

1. Pezani mau amodzi otanthauza mau angapo awa:-
   Citsanzo: Dzuwa liwamba mtengo – Msana.
   Mfiti zitamba –
   Nkhuku zilowa –
   Nkhuku zilira –
   Pansi pali mbu! –
   Ati nagona pano –
   Pezani mau ena m'nkhaniyi.

## MAU WOPATSA MAGANIZO

2. Palibe malo ena woposa kwathu.

3. Pogwirizana ndi aphunzitsi pezani mbiri ya midzi yozungulira sukulu yanu.

i ya midzi

## PHUNZIRO 3

### NSANJE

Nsanje ndi khalidwe losakhutira ndi zinthu zako uli nazo. Mtima wakaduka wosafuna wina kukhala ndi zinthu zabwino. Mtima wofuna zonse zabwino kuti zikhale zake. Mnzake akakhala nazo amayesetsa kuti zimcoke m'manja mwake ndipo kukaterodi, amakondwa namanena kuti tafanana kaya amati atani. Khalidwe la nsanje ndi laumbombo, lofuna zonse zikomere iye. Pakanthu kali konse akhumba iye akhale woposa anzake. Nthawi zonse nsanje imaonetsa mbali yoipa ya cinthu. Munthu wansanje amafuna kulanda cinthu wapeza kale mnzake. Safuna kupeza cina cake yekha colingana ndi ca mnzake uja ai. Sakonda kuti akhale naco anthu awiri. Awopa kupikisana. Ncifukwa cake afuna amlande mnzake kuti akhale naco yekha.

Mtima wansanje sukhala mwa mtundu umodzi ai. Upezeka pakati pa mitundu yonse ya dziko lapansi. Ilibe uyu ndi mwana kapena wamkulu, wolemera kaya wosauka, wophunzira kapena bubu, mnansi kaya m'nthudera, nsanje n'cikwane-kwane ngati dzuwa lowala pali ponse. Tsono mtima wanjiru wotere, ucitika pa nchito m'banja ndi pena pali ponse pali anthu. Mwacitsanzo, pali anthu ena akaduka ndi ana anzawo. M'malo molanga wake mwana, aganiza zoononga mwana wamnzake cifukwa coti agwira pamimba kwambiri makolo ake. Amdyetsa bwalero kapena kafere kwanu. Mtima wam'phera njiru ndipo adziwa kuti palibe phindu kwa iye. Kaya munthu wina amene alibe ndi zomuyene-

retsa kukhala udindo wakuti wakuti, cifukwa ca kaduka kacinangwa, sapeza mtendere mumtima mwake mpaka atamgwetsa mnzakeyo. Atamgwetsa, kwake kumtima zii! ali namcotsa ng'ala. Nanga wapindulanji? Sangathe kukhalapo pampando wasiya mnzake uja, ndipo ngakhale kuufunditsa kumene. Sangathe. Tsono tiona kuti nsanje zotsatira zake ndikubvutitsa anzake cifukwa ca zinthu zawo. Komanso nthawi zina munthu wakaduka, amatha kuswa zinthu zaeni zamtengo wapatali zimene sazidziwa nchito yake. Cocitira ndi mtima watifanane basi. Samvetsa kuti aliyense alandire ulemu ndi zinthu zake ai. Iye kwake nkuwanditsa mbiri yonama kuti wakuti wakuti anyang'wa cifukwa ca cakuti cakuti. Sanawamve nalankhula, koma angosemeramo zifukwa zake cifukwa ca mtima wansanje. Gulu la anthu ena limati, nsanje ndi kusirira ndiponso ndi cikondi. Inde, nawonso anena m'tinthu. Sitingatsutsiretu maganizo awo, popeza maganizo amnzako nkamba wake, samdyera. Tsono maganizo awo ndi wotere:-

Coyamba kucita munthu mtima wankhwidzi usanazike mizu mumtima mwake, ayamba kusirira. Akhala ndi ganizo lakuti ici ncabwino ndipo cikadayenera iye. Ndipo akawolowera kuti usiriro ucite ufumu mumtima mwake, mtima wake umasinthika ndipo zocita ndi maganizo ake amakhala osiyana konse konse ndi akale. Coyamba, mumtima mwake sakondwera n'pang'ono ponse poganizira cinthu cimene afuna. Komanso coipitsitsa kwambiri ndikuti ayamba kumuda mwini cinthuco. Caciwiri, amayesa kuti m'mene iye alibe, kutanthauza tsoka. Sazindikira kuti Cauta amapatsa madalitso mosiyana. Kwake nkunyoza gawo lake anampatsa Mlengi. Aganiza anamumanira dala. Ncifukwa cake alimbana ndi munthu amene analandira, kuti amlande kapena amuonongere, afanane.

Tsono malire yeni-yeni yolekanitsa nsanje ndi kusirira

ali apa. Nsanje ndi kaduka kacinangwa pamene kusirira kuli kaduka kambatata. Paja mudziwa kuti cinangwa cikadukira siciphukira. Cimaola. Koma mbatata ikadukira posakhalitsa pamatuluka ciphukira. Nsanje wake ndi undekha, kulanda cinthu camwini, kuti asakhale naconso ai. Mwini cinthuco abvutike basi. Ndi khalidweli, palibe kuganiza kuti munthu atha kupeza cakuti ciri ndi ngana atachera thukuta naye. Koma kwake ndikufuna kulanda cimene mnzake anagwira kale. Munthu wotero alibe mtima wofunsa kuti ici munacipeza kuti ndipo mwanjira yanji? Alibe. Khalidwe lake ndikuonera m'madzi mwini cinthuco ndi mtima wakuti sicimuyenera, koma ciyenera ine. Kusirira kusiyana ndi nsanje pang'ono, cifukwa pali kusirira kwina koipa ndipo kwina kusirira kwabwino.

Kusirira koipako kufanana ndi nsanje. Kusirira kwa nsanje ndi pamene kusirirako kufika pa mtima wofuna kulanda zamwini. Ndipo kusirira kwabwino ndikukhumbira cabe. Mtima ukafunitsa cinthuco, amafunsa kumene anacipeza ndi m'mene anacipezera. Kaya tifanizire kuti munthu wina wapenya mkazi wamwini wokongola ndipo wamakhalidwe wokoma ndi wokhumbirika, ayamba kumsirira. Tsono kumtima kukakhala usiriro wansanje, maganizo abwera yoti mkaziyo samuyenera mwini wake koma akadayenera iye. Ndipo ndi ganizo lotero, ayamba kuponda zidendene mwini mkazi, pomunyengera kuti amlande. Ngati mkazi abvomera, paja adati, gona ndi mwini nyumba, amuveretsa m'maso, pomtengera nkhali yake. Ndipo ngati mkazi uja amkana munthuyo, aganiza zomlumaza. Ndipo mwina amamlumazadi. Uwu ndi usiriro wansanje. Koma kusirira kwabwino kumatere; munthu wosirirayo amapita kwa mwamuna wa mkaziyo, namfunsa m'mene anampezera mkazi wabwino wotero. Atamva, naye amalowa m'thengo soka soka! kudula mtsitsi ndi mano

kuti apeze wake. Tsono akacita mphumi, amampeza. Ngati wakhumbira nsalu ya mkaziyo, safuna kulanda mkazi wamwini cifukwa cobvala nsalu yabwino ai, kwake nkufunsa kumene anagula nsaluyo kuti nayenso akagulire mkazi wake. Munthu wosirira mwa mtundu uwu, amazindikira kuti kanthu sikabwera kokha kaopa ulaula. Azindikira kuti cabwino cibwera kwa munthu pamene akudya thukuta la pankhope pake.

Gulu lina limati nsanje maka ngati ikhudza ku cibwenzi kapena ukwati, isonyeza cikondi. Anthu ambiri amati, 'pali cikondi pali nsanje'. Nsanje-cikondi itanthauza kuti mwini bwenzi safuna bwenzi lake kuceza ndi anzake amene mwina akhoza kukhala ndipsyi, cifukwa akana kulirira kuutsi. Afanizira bwenzi lija ndi munda wa cimanga wokhala pamtetete, poti ziweto zikhoza kubvubvutamo. Tsono nsanje yake ikhala chinga, lochingira munda kuti ziweto zingaononge. Koma poyang'ana mbali ina ya nsanje – cikondi, isonyeza kusakhulupirirana pakati pa abwenziwo. Sazindikira kuti munthu ndi munda nzolekana.

Munthu ali ndi nzeru zodziwira zoipa ndi zabwino, zokhozeka ndi zolakwa. Ziweto nkutheka kuononga cimanga. Koma munthu ali ndi maganizo ake ake. Munthu ali ndi pakamwa pokanira. Pokha ngati abvomera, cibwenzi cikhoza ubvubvutika cifukwa, fundako ndi mwini bulangete. Mlendo sadandaula ngakhale amfundikeko mphonje zokha zabulangete. Cabwino, funso nali, mutapeza panyumba yanu munthu ali kuthawa ndi njinga yanu ndipo wina watenga cikumu mkazi wanu, kodi mungayambe kuthamangira ciani?

1.
2.
3.
4.
5.
6.
7.
1.

## KUMVETSA NKHANI

1. Kodi nsanje nciani?
2. Kodi gwero la nsanje ndiliti?
3. Amacita nsanje kwambiri ndani?
4. Kodi mlembi asiyanitsa bwanji nsanje ndi kusirira?
5. Kodi nsanje-cikondi njabwino? Perekani zifukwa zitatu.
6. Kusirira kokhumbira ndi kwa nsanje kusiyana poti?
7. Yankhani mopereka zifukwa zokwanira funso lotsiriza la nkhaniyi.

## KUPHUNZIRA CILANKHULIDWE

1. Pezani maina ya aneni awa:-

| Citsanzo:- *mneni* | *maina* | |
|---|---|---|
| kolola | kholola | zokolola |
| chinga | ..... | ..... |
| dyola | ..... | ..... |
| manga | ..... | ..... |
| chedzera | ..... | ..... |
| kuntha | ..... | ..... |
| sangalala | ..... | ..... |
| tema | ..... | ..... |
| duwa | ..... | ..... |
| khumba | ..... | ..... |

Aneni ena ali ndi maina awiri:-
Kuntha(i)khuntho – sefa wa mowa.
(ii)mkuntho – kuomba kwa mphepo.
Pezani aneni ena ndi maina awo.

## MAU WOPATSA MAGANIZO

2. Nsanje simanga mudzi

## ZOKAMBIRANA

3. Kambiranani pa mitu ya nkhani zotsatirazi popereka zifukwa zomveka.
   (i) Pali nsanje pali cikondi.
   (ii) Nsanje ndi khalidwe limene lipezeka mwa munthu amene aganiza za kulephera kwake kopezera zakuti zakuti, zimene ziri ndi wakuti wakuti.

## PHUNZIRO 4

### MWAI NDI TSOKA

Mwai ndi tsoka ndi ana amapasa, ayendera limodzi. Ena amati ndi agumu awiri a pa phesi limodzi, kaya munthu ndi cithunzi-thunzi cake, cifukwa nthawi zonse zilondolana. Mwai ndi tsoka zimakhala ngati cinthu caphanthi, cokhala ndi makhwakhwa awiri osiyana. Malembo a pakhwakhwa lina akuti mwai ndipo a khwakhwa linzake akuti tsoka, koma onse ali pa cinthu cimodzi. Wosimba mwai amasekera cifukwa asonyeza kupambana kumene kwa wononga mnzake. Ndipo watsoka amalira ndi cisoni cifukwa walephera cinthu anacifunitsa. Inde, masiku ambiri tsoka sasimba mwini wake, mwina akhala atafa kale. Mwai sukhala mwai nthawi zonse kwa munthu cifukwa umasinthika kutsatana ndi colinga cake. Ndipo tsoka silikhala tsoka nthawi zonse cifukwa nthawi zina tsoka lako limakhala mwai wako.

Tsono mosataya nthawi, tiyeni tione zitsanzo zina zolongosola tsoka ndi mwai. Pamudzi wina panali mkazi dzina lake Liyana amene cikondi cake cinakangamira mnyamata dzina lake Phoso ngati litsiro. Ndipo Liyana anali kunena mopanda mbiso kuti akonda Phoso ngati nsima. Cinalidi cikondi cankhunda, samatayana koma anali ngati mbewa ndi mcira wake. Masiku a ukwati atafupikirana ngati pakamwa n'pamphuno, mwamuna anasintha maganizo ake. Anaona mkazi wina dzina lake Tiyese, amene anthu amasimba kuti ndi thatha, wogwa

nciswe. Mbiri ya cibwenzi ca Phoso ndi Tiyese itagwa m'makutu Liyana inamuthyola m'nkhongono, nalira kuti wacita tsoka. Anamva cisoni nati, wafera m'khomo m'nyumba mosalowa. Komabe analimba mtima pozindikira kuti cikuni cimataya ndiwo zopsyaipsya. Tiyese uja anaimba nyimbo ya nadala, namati wamsambitsa cokweza mnzake uja Liyana koma osadziwa kuti wayamika wamoto.

Khale-khale yauka ndeu yamkati mwananama. Nayo nkhonya yapakamwa gumu! mano ya Tiyese poti alabvule malobvu, mano mbwe! pansi. Analira 'Mayo ndinayesanji ine'. M'mawa agalamuke, mano a pamphumi pali ng'wa! maso alowa mkati ngati olumidwa ndi njuci. Nanga mkazi wamwai ndi uti? Woyamba akuti ali ndi mwai ndipo waciwiri asimba tsoka.

Mucitsanzo cina, James ndi Zakoupanira ayimba sukulu limodzi. James anaphwanya mandala ya mphunzitsi ndipo abisa. Tsiku lina Zakoupanira anangocita ngati amlodza, kaya cifukwa comuipira m'maso, am'neneza kuti mandala ya mphunzitsi anaswa ndiye. Mphunzitsi ndi mkwiyo wonse, anamgwira Zakoupanira ndi kumtibula kwambiri mpaka kukomoka. James anasimba mwai cifukwa anapulumuka kwa mphunzitsi. Nthawi yomweyo, Zakoupanira, amcotsa sukulu. Anzake onse anati Zako ali ndi tsoka, sadzadyera dziko.

Zako ali kumudzi, anaphika mutu ndipo anayamba timalonda tosadziwika bwino. Patatha zaka ziwiri, anamanga sitolo, nagula galimoto ndipo anzake aja anamseka kusukulu, aomba m'manja kwake kufunsa ngongole. Zako anayamika kucotsedwa kusukulu kuja cifukwa akadapanda kumunamizira kuti ndiye

waononga magalasi ya mphunzitsi, sakadakhala monga m'mene aliri. Nanga tsoka n'liti?

Mwai kapena tsoka ligwera m'modzi kaya gulu ndipo zimapatula pa gulu lina. Citsanzo, munthu wochuka kwambiri, anaitanidwa kukalankhula pa cimsonkhano ca nthumwi zambiri zocokera ku dziko lonse lapansi. Malo yake mundege yopatulika anakonzeratu. Litakwana tsiku ndi nthawi, anadabwa pamene malo ake m'ndege muja ataikapo munthu wamba. Anakwiya, nalalata ndipo anafuna kudziwa kumene kwacokera mnyozo wotero. Koma wolongosola za mayendedwe a ndege anayankha ndi mau awiri okha, 'mupita mawa'. Ndege inauluka, iye poti akwere m'galimoto kubwerera kunyumba, anaona mwendo umodzi waphwa. Poti aikeko mwendo wina, nkanthawi ndithu. Ndipo patapita mphindi zowerengeka anamva kwa andege anamuuza aja, kuti ndege ija yagwa ndipo anthu wonse atha cipere Atamva, m'nkhongono munasuti weye.! weye! nayamba kudzilirira. Anasimba mwai.

Tsono pomaliza pali nkhani yotere:- Mnyamata wina anacoka kumudzi kufuna nchito m'tauni. Anayenda tsiku lonse kufunsa apa ndi yapo, koma nchito yosapezeka. Dzuwa litapendeka ndithu, njala inamuwawa ngati cironda ndipo nimufoketsa. Anayamba waleka kufuna nchito, nayamba kupempha cakudya. Anayesa muno, koma popanda wompatsa kanthu. Anayenda moguzika napumula patsinde pamtengo. Usiku, nyumba zonse zogulitsiramo cakudya atatseka, anacoka pamtengo uja. Kukhosi kunauma gwa! kuthira malobvu amangogwa pamtima. Tsono anaganiza zosuta fodya. Ndipo asanazinge ndudu, anapatuka kuthira mvula. Mwendo wina unaponda cikalakala. Atatha kutaya madzi, anatola cikalakala cija kuti azingire ndudu. Popenyetsetsa

anaona kuti ndi pepala la makwacha asanu. 'Ha! nacita mwai', anatumpha, timphamvu tinadzamo m'thupi. Mosataya nthawi anafuna-funa koti akagule cakudya, konse anatseka. Kufoka kunalowanso m'thupi lake. Mphamvu zoti nkupita kutali kokagona zinatha ndipo ndalama iri m'dzanja analowa kunsi kwa mlato kuti agone. Tsono atagona, komweko kunali upita.

M'mawa, anthu wopita m'njira anaona miyendo ya munthu kunsi kwa mlato. Wosakhalitsa a polisi anafika, namsolola naona kuti wadziumira tsungwa, koma ndalama ija yosacoka m'dzanja. Pompenyetsetsa, apenya kumimba kuli bebekhu! kumimba ndi kumsana kwaombana. Pomwepo anazindikira kuti wafa ndi njala. Uwu ndi mwai-tsoka wotola ndalama masitolo atatseka. Ukagula kuti?

Munthu aliyense atsata njira ya moyo wake imene inalongosoka kale. Saidziwa koma iripo. Ambiri amadandaula kuti ine ndine watsoka cifukwa anandipatsa tsoka ndi uje. Sazindikira kuti mwai wamnzako ndi tsoka la wina. Wotaya kanthu akuti wacita tsoka, koma wotola, athokoza kuti Cauta ali naye.

## KUMVETSA NKHANI

1. Fotokozani kusiyana kwa tsoka ndi mwai.
2. Kodi pa ukwati wa Liyana anali ndi mwai ndani?
3. Kodi mwai umadziwika? Pezani zitsanzo kwa Zakoupanira ndi mlendo wa pandege.
4. Nanga mwai-tsoka umatani?
5. Tsono pezani tsoka ndi mwai mokha kucokera m'nkhani zonsezi.

## KUPHUNZIRA CILANKHULIDWE

1. Mau wosowa m'ziganizo za gawo (a) apezeka m'gawo (b):

*Gawo (A)*

(i) Mwana apita naye kucipatala cifukwa.....

(ii) Mudzi wa a Nyama waonongeka ndi.....

(iii) Yona ali.....pamene Kontho anapita ku Ulaya.

(iv) Pali..... pakati pa Ng'oma ndi Nambewe.

(v) Ika dengu lako pa.....

*Gawo (B)*

phampha, kabvuwe-bvuwe, wafundidwa m'thupi, kufunditsa mpando, cikondi cankhunda.

## CIPHIPHIRITSO

2. Mwai n'tsoka lomwe.
Mwai wa ukundaleka.

## ZOKAMBIRANA

3. Kambirananani ndipo siyanitsani ziphiphiritso izi;-

(i) Cikuni citaya ndiwo zopsyaipsya.

(ii) Pafupi ndi apo wafika.

4. Mwai unandigwera tsiku lina.

## PHUNZIRO 5

## COIPA CITSATA MWINI

Pamudzi wina panali abale awiri ndi alongo awo atatu. Mbale wamkulu anali wamtali koma wamfupi nzeru. Anthu ambiri anali kuti ndi wamtali ngati makanja ndipo ena amati ngwamtali ngati sungwi. Anali wokulupala bwino ndipo maso ake wowala ngati a cona. Khalidwe lake linali losakondweretsa anansi ake. Amapsya mtima msanga ndipo ndi mtima wa dzimbu, anali kulalata, kutafula ndi kuopsyeza. Tsono cifukwa ca thafu lake, anali kumuda anansi ake. Ndipo m'ng'ono wake wobadwa naye mimba imodzi, anali wosiyana konse ndi mkulu wake. Anali wamfupi kopyolera muyeso. Ndipo atsikana omcedzera, anali kumucha kuti ndi kabwata kufanizira mtundu wa nkhuku yamsinkhu waung'ono. Koma khalidwe lake linali labwino, motero kuti alongo ake onse ankagonera pa iye. Cifukwa ca msinkhu ndi khalidwe, anthu anali kuti zoona kuti m'mimba ndi m'ng'anjo.

Caka cina wamkulu uja anapita ku ulendo ukagwira nchito. Anakagwiradi ndi mphamvu motero kuti zolira mtima wake anazipeza. Pobwerera m'njira, anali ndi ganizo loti sakapatsako acinansi ake cifukwa amamuda. Atafika, mbumba yonse inasekera kuti ilandira kanthu, koma osadziwa kuti wasekera fupa wayesa mnofu. Ndipo zedi, sanapatseko n'nena m'pang'ono ponse. Inde, ngakhale ndi kamceka komwe komanga mciuno. Anawamaniratu. Anaumadi mtima, samazindikira kuti masiku amatsutsa cifukwa amatha ubweya wa nguwo.

Tsiku lina, mtima utalasa phaso, ndipo akulu akale adati, mtima udawawa galu, m'ng'ono wake anapita ku nchito kukana kubvutana ndi mkulu wake. Popeza anapita n'colinga cotha umphawi wa banja lonse, anakhwimiriradi. Ndipo anagula zobvala zokwanira aliyense. Nayenso anasokoloka kumudzi patatha zaka ziwiri. Atamulonjera, anauza mbumba yake ndi mbale wake yemwe kuti abwere tsiku lakuti adzawagawire zobvala. Patsiku logawa, kunali cimwemwe codzala tsaya. Phwete losacoka pakamwa. Aliyense analandira, kupatula mkulu wake yekha. Bokosi atatseka, mkulu uja anafunsa ngati wamuiwala. M'ng'ono wake anang'una, aliponi duu! osayankha. Ndipo atafunsanso, wam'ng'ono uja anayankha kuti akumbuke zadzana. 'Zadzana zotani?' anakalipa. 'Pepani mkulu wanga.' anayankha uja, 'Lende nkukankhana. Ndipo ucembere nkudyerana.' Tsono ndi mau awa, mkulu uja anagwa ngololo. Mbumba nazo zinayamba kuwatukwana akulu aja cifukwa ca kuuma mtima kwawo. Mkulu uja anatuluka m'nyumbamo mtima uli psyu! Anali omvetsadi cisoni cifukwa nthawi imeneyi kambuku anali atakhala kwambiri kumsana.

Usiku wonse mkulu uja anagona mwa ciphupha moyo cifukwa ca mnyozo analandira kwa mbumba yake. Sanadzione kuipa kwake, cifukwa kanyimbi sadzimva kununkha. Mkulu uja anada m'ng'ono wake, ndipodi anamuda. Sanafune kuonanso nkhope ya mbale wake. Inamuipira. Usiku womwewo anayamba kuganiza njira yophera mbale wake. 'Kuti mbumba yanga iyanje ine,' anatero mkulu uja, 'mwana ameneyu afe basi kuti mbumbayi isowe mdowero.' Atatsimikiza zakupha mbale wake, anaganiza zamalo ndi woti nkumuphera mopanda cifundo. Malo ake anawapeza ndiko kucikamwini kwake.

M'mawa kutaca, mkulu uja anadza kwa m'ng'ono

wake atabisa mkwiyo wonse kuseri kwa mano ake woyera. Anali munthu woseka ndi mano, koma osati phwete la kumtima ai. Makambidwe anasintha, anali kukamba mofatsa ndi mwaciphimba m'maso. Bwino lake mkulu uja anapempha mbale wake kuti apite naye kwawo akamuone alamu ake amene sanapeze mpata wodzamuonera. Iye anabvomera kupita naye limodzi.

Tsiku litafika, ananyamuka ulendo wa kuimfa. Kwa mkulu uja colinga ca ulendowo cinali kadziwa mwini mkhuto wa fulu koma kwa mbale wake unali mphuno salota. Anangonyamukiramo m'cimutu-mutu. Mbwe! Padambo pena, anapeza munthu agulitsa nsomba zamatumbi. Mnyamata wa ku ulendo anagulako. Atayenda kamtunda ndithu, anamva kununkha kwake ndipo mosafunsa mkulu uja anazitaya kuthengo khwefe! Pamudzi wina pafupi ndi cikhute camowa, anapeza munthu wina agulitsa zitsenda. Anagulako. Ndipo atayenda pang'ono, anamva kafungo kamphukusi muja kali yepi! koipa. Anaziwaza kuthengo. Zonsezi kwa mkulu wake uja zinali kuonjezera canzi kununkha. Panjira pena anakumana ndi munthu atasenza cipungu, nacitsatsa malonda. Mnyamata uja anagula. Mkulu poopa kuti atayanso, anafunsa kuti anyamule ndiye, mbale wake anakana cifukwa wam'ng'ono ndiye a-nyamula katundu ngati ali pa ulendo. Mkulu uja anangoti dukwe! usowa colandula. Atayandikiza kufika, anacitayanso cimbalame cija. Potaya, mkulu uja anampenyetsa ndi diso la nkhwezule. M'njira monse amayenda ndi kutaya zinthu amacita mbale wake, amakucha kunyang'wa ndi ndalama. Dzuwa litapendeka, anafika ku cikamwini kwake.

Wonse anagona tulo tabwino, kupatula mkulu uja amene anagona mutu uli kukhomo. Usiku wonse osagona kumangoti kuce msanga ndi mlembere waganyu mbale wanga amukonkhonthe. Ali pabwalo ndi anthu

analemba ganyu aja, analonjeza anthu kuti mbale wake ali ndi cuma cambiri cakuti nkudzaza madengu onse a pamudzi paja. Ndipo anati ngati sadzaza amuphe. Madzulo anthu anaunjika madengu pakhomo panyumba imene amagonamo mlendo kuti m'mawa apeze odzala ndi ndalama. Ndipo ali mkati mwa cidandaulo, pakhomo panamveka mau. Atatsegula, nsomba zinamtsitsa moyo pomuuza kuti apale mamba yawo ndipo asanduka ndalama. Anapala, ndipo m'mawa, anthu onse anagwira pakamwa poona cuma. Ali pabwalonso tsiku lina, anauza anthu kuti mbale wake akhoza kugwetsa cimtengo cacikulu cija coti anthu khumi atagwirana manja sangathe kuuzungulira. Ndipo anati akadule m'mawa mwake.

Usiku atagona, ali m'madandaulo, zitsenda zinagogoda pacitseko. Potuluka, zinamuuza kuti zimuthandiza kudula mtengowo. Anapitira limodzi usiku nzimulozera poti akadule mtengowo. Kutaca, gulu linamutsata. Atafika pacimtengoco, monyada, anadula cimtengo cija. Ndipo ndi nkhwangwa imodzi cinagwa kuti phii! Anthu anakondwera koma mkulu wake sanakondwere cifukwa ankafuna afe ndithu. Tsono ali kucezanso, anapekanso bodza lina ndipo anati, 'Mbale wangayu, mfumu mutampatsa mkazi lero akhoza kubereka mwana ndipo mawa mfumu mwanayo akhoza ukuphikirani nsima. Ngati akanike konzani.' Mfumu sinataye nthawi, inafuna mtsikana wowoneka ku anthu. Ndipo madzulo inawatsekera m'nyumba kuti awapeze m'mawa.

Nthawi iyi mnyamata analira. Ali nkuiira, anamva pakhomo gogogogo! Atuluke, wakumana ndi cipungu cija, 'Uliranji bwenzi langa?' cinafunsa cipungu. Molira anayesa kulongosola kuti apa n'pomwera ndipo apo n'posamba. Cinamuuza nati, 'Osadandaula, nzapafupi.' Cipungu cinapita kwina kutali ndipo cinapeza atsikana

ena nasewera. Cinangoti pa m'modzi phii! Katsu! Thubvu! cakatsula. Pacitseko gogogogo! Citseko tseku! ciliponi mwana suyu! Mnyamata uja mtima zii! aliponi gonu! kupha tulo. M'mawa anthu anadzala pakhomo, dzuwa pamwamba asanadzuke. Pano ndi potuluka, anatuluka nakankha nkhongo ya mtsikana, mwana anabereka, amene anaphikira nsima mfumu tsiku lija. Ndipo dzina la mnyamata uja linakhala m'kamwa mwa aliyense tsiku lija. Koma kwa mkulu uja, lake linali tsembwe cifukwa cakulephera kwake.

Isono munthu ukacenjera pogona, mnzako amacenjera pouka. Kunaterodi. Atakhala pabwalo paja, mbale wake anauza mfumu kuti mkulu wake akhoza kugwetsa nyumba yanjerwa ya mfumu ndi kuimanganso tsiku lomwero, nigonamo. Mfumu inabvomera ndipo m'mawa mkulu uja anayamba kucotsa malata. Dzuwa linafika pakati pamutu asanathe kucotsa malata. Litapendeka dzuwa, anayamba kusolola njera imodzi imodzi mpaka dzuwa tswii! Waononga nyumba yamfumu. Ndipo monga mwalonjezo, anthu anamkoza iye. Anadziphetsa cifukwa ca nkhwidzi ndi mbale wake.

## KUMVETSA NKHANI

1. Kodi abale awiriwa anali kusiyana bwanji?
   (i) M'maonekedwe (ii) M'macitidwe?
2. Bwanji wam'ng'ono atabwera ku ulendo anaonetsa khalidwe lija kwa anansi ake ndi mkulu wake?
3. Kodi wamkulu uja anafuna kumupha mbale wake cifukwa ninji?
4. Anatsata njira yanji?
5. Muganiza mbale wake anapulumuka cifukwa ninji?

## KUPHUNZIRA CILANKHULIDWE

1. Phunzirani mau awa ndipo pangani ziganizo zanu pogwiritsa nchito mauwa:-
kulupala; khwimirira; nkhwidzi; kuphika mutu; yanja; bvumata; cagada; penda; ngana; m'nthudera; nzankhani.
Pezani ziyenerekezo za zinthu izi:-
Citsanzo: Wamtali ngati makanja (cirombo)
Wamtali ngati ..... (udzu)
Kuda ngati ..... (mphika)
Mtonkhatonkha monga ..... (galu)
Ufupi ngati ..... (nkhuku)
Kubiriwira ngati ..... (udzu)
Tsono pezani zina mokha.

Ziphiphiritso zambiri m'Cichewa zicokera m'macitidwe ya anthu ndi zinthu zina. Citsanzo: *Kugwa ngololo* kumene kutanthauza *kutha mphamvu*. Mau awa acokera ku nyama ija yochedwa nungu. Ngololo ndi minga zimene zipanga citsukwa ca nungu. Imadziteteza poponya minga kwa adani ake. Tsono ikagwetsa ngololo ndiye kuti yalema, yatha mphamvu ndipo iri pafupi kufa. Nanga mau awa akhudzana ndi ciani ndipo atanthauza ciani?

| *Mau* | *Tanthauzo* | *Gwero* |
|---|---|---|
| Kugwa ngololo | kutha mphamvu | Nungu (Nyama) |
| Kuutsa cenjerere | ..... | |
| Kupsyatira mcira | ..... | |
| Kupukusa mutu | ..... | |
| M'mimba ndi m'cipala | ..... | |

Yamika wamoto .....
Pezani mau ena.

## CIPHIPHIRITSO

2. Galu wamsala aluma mwini.

## ZOKAMBIRANA

3. Mopereka zitsanzo munaona, bvomerezani kapena kanani za coipa citsata mwini.

## PHUNZIRO 6

## KULUZI

Ku zambwe kwa dziko lina kunali cinkhalango cacikulu mu utali ndi mu ufupi momwe. Panalibe wodziwa kukula kwake kuti ndi mitunda ingati cifukwa munalibe miseu ya magalimoto ndiponso anthu masiku amenewo, analibe zoyesera mitunda. Poyesa kutalika kwake, ankayesa moyendamo pansi kucokera m'mudzi wa mbali yina kukatulukira ku mudzi wa mbali yinanso. Ndipo amati munthu wodziwa kupalasula pansi atacoka mbali yina tambala m'modzi, anali kutulukira mudzi winawo ndi kacisisira. Koma anzanga ndiine, osadziwa kupha nyerere, anali kugona m'nkhalango momwemo. Tsono dzina la cinkhalango cimeneci, coopsya cifukwa

ca nyama za mtundu-mtundu ndipo zina zodya anthu, linali Katayamoyo.

Ndipo cifukwa ca kuopsya kwake, maka pokhalamo nyama zolusa ndiponso akulu ankati m'menemo ndimo munali kugona azimu, samalola anthu kusakamo. Kunali koletsedwa. Koma ngakhale kunali koletsedwa, anthu adobvu ndi ugonthi, sankazigwiritsa nchito zokamba akulu zija. Anali kupitako kukasaka nyama. Tsono poti akulu angadziwe, anapeka mau awo wokabera nyamazo, ndipo amati, 'Kukasenda Luzi' ndipo cidule ankati 'Kuluzi'. Luzi la kumeneko linali la mtengo wa mombo. Limakhala lofiira lalitali, amalikulunga mitolo-mitolo ndipo nthawi zina anali kuzinga nkhata. Maonekedwe ake patali, limakhala lofiira ngati mzongo wa nyama. Komanso anthu amakasenda luzi ku nkhalango yomweyo.

Tsiku lina mlenje wina wa kwa Kamzati dzina lake Chimfuti, anapangana ndi anzake zopita kuluzi. Atakambirana masiku angapo, anapangana tsiku lonyamukira. Ndipo patsiku lonyamukira, Chimfuti anacita mtopola ndi mkazi wake woyamba. Anayambana cifukwa Chimfuti sanasamale masiku woyenderera mitala yake. Anataya masiku ku mkazi wake wa mbaye, ndipo mkazi wamkulu anafuna udziwa cotayira dongosolo la ukwati wao. Chimfuti sanafune kulongolozana ndi mkazi ndipo popeza anali ndi mtima wapacala, anakankha mkazi wake namubwanyula. Poti afunsenso mkazi, yamugwa kale malobvu kumaso. Koma cowawitsa moyo kwambiri, ndi mabweredwe a mkazi mnzake, amene anatuluka m'nyumba ndi mthiko kuti akunkhunthe nawo mnzake. Anazaza nati, 'Bwanji ulondola mwamuna kuno kunyumba kwanga monga ndi wako wekha? Nikukunkhuntha lero, sindingaope mnzanga

wabere.' Koma mkazi wamkulu moleza mtima ndipo natsangula malobvu pankhope, anayankha nati, 'Kwanga sikudzakulanda ndoda yathuyi ai, koma ndifuna kufunsa cimene cinalepheretsa dzulo kulongosola mayendetsedwe awo a mitala. Ndiponso sindifuna kuzokozana ndiiwe mnzanga wa mkazi ai. Ife ndife amodzi cifukwa mwamuna wathu ndi m'modzi. Komanso dziwa kuti nsanje njoipa cifukwa ife akazi ndife maluwa. Ine ndiri mtsikana ankandikonda kwambiri, koma lero cifukwa ndinacembeza, ada nane kukhosi, ndimo anatengera iwe. Tsono sikale ufwifwe, ndipo ukafwifwa, atenganso wina mnzathu. Nanga iwe udzatani?'

Mai wa Chimfuti anadza modandaula naombetsa manja m'makwapa nati, 'Kwagwanji m'mawa ngati uno? Kwagwanji?' 'Nanunso amai talekani kufunsa,' anatero Chimfuti kutsekereza mai wake. Pokana kuyankha mafunso a mai wake, anauza anzake kuti anyamuke ulendo wawo tsiku lomwero. Pano mai wake anamkaniza kuti asapite ku ulendo cifukwa ukhale ulendo watsoka. Koma Chimfuti anauza mai wake kuti sangagwiritse nchito maganizo ya anthu akale, cifukwa izo zinatha ndi ukale wake. Akulu akale adati, tsobola wakale sawawa. Ndipo mai wake anati, mau akulu akoma akagonera ndiponso dziwa mwana wanga kuti pocoka ulendo usamacoka moduwa. Ukatero ndiye kuti ulendo ukhala wobvuta kwambiri. Cinanso, pamudzi utacoka utadya nsima ndiwo ndi nyama, kuli konse uyende udzadya ndiwo zabwino. Koma ngati ucoka ndi njala, yako ndi njala yokha-yokha. Ulibe mwai. Chimfuti anauza mai wake kuti amenewo anali maganizo opusa ndi opanda nzeru. Ndipo mosataya nthawi anapita kunyumba ya mkazi wake wamkulu natenga mfuti ndipo womwewo unali ulendo wa kuluzi.

Anayenda ulendo wautali ndithu, naona ndowe ndi mapazi a njobvu, magulu a mbidzi ndi nyama zina. Sanafune kulasapo nyama zija cifukwa mfuti ikalira, imamveka kutali tsono samafuna kuti anthu amve kulira kwa mfuti yake. Atayenda ndithu, anasankha cigono cao m'kati, m'makwete-kwete a m'mbali mwa phiri. Anali malo ogona, osungirapo zofunda, ufa ndi nyama yowamba-wamba. M'mawa, mlenje ndi anthu ena, anapita kufuna njobvu, cifukwa ndiyo inali nyama yamtupatupa. Anayenda dzuwa lonse osaipisa m'maso njobvu. Mapazi nindowe anazipeza apo ndi apo ndipo pena anali kupeza ndowe yofunda, nayembekeza kuti mwina zinali pafupi. Polondola njira za njobvu zosiyana-siyana, ndikuyenda m'malo acifani-fani, anasokera. Anayesa kukuwa, koma kucigono kuja kunali kutali kwambiri moti mifuwu yawo sinamveke. Tsono anakwera m'mitengo nadzimangirira ndi luzi nagona tulo.

Ndipo usiku anyamata anatsalira pacigono paja, sanatinyanthe tulo n'pang'ono pomwe. Kaya mwina anagona popeza tulo ndi nkhondo tinagonetsa wolira. Usiku wonse anabvutika mtima ndi mantha pamene mikango inali kutsika m'phiri kupita ca ku cigono kwawo. Mukamsasa anakhalamo, anangomamatirana ngati njuci panthenje yake. Kugunda kwa mitima yawo kunali kumveka ngati mgugu wa mapazi ya anthu ndipo mwina ngati mgundu wa mtondo. Aliyense anali kuda mnzake kuti kugunda kwa mtima wake kuwaululitsa ndi kuwadyewetsa. Ndipo anakhala coundana conco usiku wonse. Mosayembekezeka anaona kwayera kubwalo kuti mbee! Tsono iwo anasuti ngwa! ngwa! ngwa! ngwa!

Dzuwa litafunda, mlenje ndi anzake anatulukira pacigonopo. Anyamata wotsalawo anafotokoza m'mene akanadyewera usiku ndi mikango. Ndipo ananena kuti

sadzayesera kutsalanso koma aziyendera nawo limodzi. Cifukwa ca liuma lawo, mlenje anayamba kuwapatsa mwambo wa nyama za kuchire. Anauza anyamata kuti nyama zam'thengo ziri za magulu awiri: Zabwino ndi zoopsya. Nyama iriyonse njoopsya ikalasidwa kupatula nyama zina zowerengeka. Tsono pafunika kukhoza mathawidwe ake. Kothawira kwake ngati nyama yakalipa ndi m'mwamba. Wina anafunsa, 'Nanga kambuku atatipitikitsa tithawirenso mu mtengo?' 'Iai,' anayankha mlenje, 'uko ndiko kudzikhweza dala. m'mwamba ndimo mwake.' Anafunsanso wina, 'Kodi mathawidwe ake nkutani?' 'Yesetsani kumuthawa mokhweta-khweta cifukwa kambuku sakhweta msanga,' anatero mlenje. 'Tsono ngati nyama ikuthamangitsani, kwererani kuseri kwa mtengo. Ici citanthauza kuti ngati mwalunjika mtengo, uzungulireni ndi kuukwerera kuseri pamene nyamayo idzagunda mtengo moulunjika.'

M'mawa gulu lonse linayamba kufuna njobvu. Ndipo atayenda mozungulira phiri lija, anapeza gulu la nyama dzina lake nsaule ziyenda mozungulirana ndipo mphongo zinali kuyenda m'mbali. Mlenje ndi gulu lake anaima nacita cidwi. Zonse zinali kuyang'ana pa culu cina pamene panaima cimkango cacikulu. Mkango unali kuopa mphongo za nsaule ndipo nthawi zina mkango umathawa polimbana nazo. Tsono iwo ataupenya, matupi anadzala madzi ndipo anacokako. M'njira alikuyenda nakambirana kuti ulendo wawo ngwa tsoka. Atatulukira m'dambo, anaona ciyendayekha wa nchefu nakungudza cikungu pena pake. Ciyendayekha ndi dzina la nyama imene imacoka pagulu la zinzake cifukwa cokalamba kapena kukhala yoposa mphamvu zinzake.

Mosataya nthawi. analeka ganizo lofuna njobvu,

ndipo ganizo loti ukayenda m'thengo wayendera zonse linadzamo. Osakhalitsa yalira mfuti kuti tibu! Mwendo wa nchefu pekete! Inathawa ganthi! ganthi! Anzake anamuuza kuti aomberenso koma iye anakana. Anawauza kuti ndi imodzi ya nyama zosaopsya. Ataithamangira, inaceuka ndipo anaona nilira misozi iri mbwe! mbwe! mbwe! ngati munthu. Mkangano unayambika, gulu lina linati aileke cifukwa imacititsa cifundo koma gulu linanso linati aitsirize ukana kuzunza zamoyo. Ndipo anati palibe kanthu ndi kulira kuja cifukwa ndi maliro m'mbale. Anaipha, namenya, nawamba nyama yake, naika m'mwamba kuti afunirepo ina.

Ndipo poti aonjezere nyama, anayenda-yenda kuti nyama iriyonse apeze aphe. M'malunje mwina anaona muli bii! popenyetsetsa anaona ndi ciyendayekha wa njati. Kumaso masinya okha okha, m'nyanga zake munamera bowa ndi mabvu anamangamo zisa. Mlenje atapenda bwino bwino, anaomba mfuti nailasa, nigwa pansi cafufumimba. Inakhala ngati yafa koma inali kupenyera m'mbali kufuna kudziwa ndani waipweteka. Ndipo Chimfuti anasendera pafupi ali ndi cimwemwe codzala tsaya. Anasekera fupa wayesa mnofu. Poti aigwire mcira, njati inauka, zangauku! yam'mata. kumpitikitsa, inali kumthamangitsa nimuminira kumsana. Tsono apita kuti ndi njati. Monse anali kuthamanga anali kulira mai ine! mai ine! kudzilira cifukwa catsoka lake. Anakumbuka zokwera m'mwamba koma anaiwala kukwerera kuseri monga mwa mwambo umene ankapereka iye. Ndipo pokumbatira mtengo, njati inamupanikiza kumtengo nimunyanyatiza kumtengo ngati cithunzi. Njati nayonso inafera pomwepo. Anzake aja anazindikira kuti yafa cifukwa

miyendo inaloza kumwamba. Awa anakhala maferano a mlenje ndi njati. Tsono anzake pobwera, ananyanyatula kumtengo mlenje uja. Anamva cisoni kuti namkungwi sanatsate mwambo. Kwa anzake, zinali ngati mau aja akuti, tsatani zonena zanga, koma osatsata zocita zanga.

Imfa ya Chimfuti inautsa mtsutso kuthengo kuja. Gulu lina linaganiza zomuika kuthengo konkuja kuti afisi kapena mbalame zidye. Koma gulu lina linakana. Linati akatero, anthu kumudzi adzati amphera dala mnzawo. Nkwabwino acinansi aziloza kuti wathu analowa apa, manda aziwapenya. Bwino lake, anamvana zoti apite nawo kumudzi. Tsono akati wafera kuti? Ndipo wafa motero cifukwa ninji? Pophika mitu, anapeza bodza lina ndiro lakuti wafera kumunda. Anampika ndipo kutada, anafika m'munda mwake ndipo wina anaomba mfuti. Mosataya nthawi anakanena kumudzi kuti Chimfuti waphedwa ndi njati kumunda. Anthu anapita nakatenga mtembo nafika nawo kumudzi. Wokatenga maliro sanayang'ane zambiri.

Potsuka maliro, anapeza luzi louma limene anamumangira. Ndipo anadabwa lauma bwanji ngati wafera kumunda madzulo womwewo. Manong'o-nong'o anayamba kuyenda mu anthu. Tsono popeza manong'o-nong'o anautsa njobvu, anzake a Chimfuti anawaika pabwalo nawapanikiza kuti anene coonadi. Anaululadi kuti anapita ku malo oletsedwa kukasaka ndipo imfa ya mnzawo inawaonekera kumeneko. Nzeru yoti mnzawo wafera kumunda inadza ndi mtima wa mantha, anaopa akulu kuwatunzula ndi kuwapusika.

## KUMVETSA NKHANI

1. Bwanji nkhalango iyi dzina lake linali Katayamoyo?
2. Kodi kukaba nyama m'nkhalangoyi ankakucha ciani ndipo cifukwa ninji?
3. Kodi muganiza inali nkhalango ya mtundu wanji?
4. Nanga tsiku la ulendo kunacitika zotani?
5. Mai wa Chimfuti anali ndi cikhulupiriro cotani pa za ulendo?
6. Nanga zofunika kutenga, kucita ndi kudziwa pa ulendo wotere zinali ciani?
7. Kodi nyama amazigawa magulu angati?
8. Fotokozani maphedwe a nchefu.
9. Fotokozani mafedwe a mlenje uja.
10. Kodi anapeza nzeru yanji yokanenera kumudzi?
11. Akulu kumudzi anazindikira bwanji kuti linali bodza?
12. Bwanji anapeka bodza lotere? Kodi anali kuopa ciani?

## KUPHUNZIRA CILANKHULIDWE

1. Pangani ziganizo ndi mau awa kutsimikiza kuti muwakhoza:- kubwanyula, mtopola, ugonthi, kunkhuntha, makwete-kwete, cafufumimba, pusika, pusitsa, mtima wapacala, wadobvu.

   Wonetsani kusivana kwa mau awa:-
   panikiza kuti anene .....
   panikiza kumtengo .....

yam'mata njuci .....
lam'mata dothi .....
pusika munthu .....
cisangalalo
cisangalatso

Mamvekedwe a zinthu ziri mu gawo (a) apezeka mu gawo (b)

*Gawo (A)*

| | | |
|---|---|---|
| mgundu, | mzizima, | mtswatswa, |
| mgugu, | mkokomo, | mthyothyo. |

*Gawo (B)*

| | | |
|---|---|---|
| masamba, | mtondo, | madzi, |
| ng'oma, ndege, | mapazi, | mphepo, madzi. |

## CIPHIPHIRITSO

2. Zakuupo zimabwera.

## ZOKAMBIRANA

3. (i) Fotokozani m'mene ciphiphiritso ciri m'mwambamu cigwirizana ndi ganizo la nkhaniyi.
(ii) Kuipa kwa kubisalira akulu.

## CIMANGIRIRO

4. Nyama zankhalango.

# PHUNZIRO 7

## MAWA

Munthu cifukwa ca nzeru zake zimene zimam'nyenga pocita cibaza kuti moyo wake ulamulidwa ndi wina, amakonda kunena za zinthu zamtsogolo. Pokamba za mtsogolo amakamba motsimikiza ndipo mau amakonda kuwagwiritsa nchito ndi mau akuti 'mawa'. Tate anena kuti mawa ndipita kukazonda matenda; mai cifukwa wagula nyama, auza ana kuti mawa atsuka m'kamwa; abwenzi awiri akonzekera kuti mawa tilowa m'banja; mphunzitsi alongosoleratu zonse zokaphunzitsira ana mawa. Ndipo pena pake ukumva anyamata a sukulu akambirana zakuti mawa asakadye cakudya ca masana cifukwa m'mbale mukhala mutanda.

Aiwala konse kuti mawa sapezeka. Ndipo mtima ungoti phii! osakumbuka mau aja akuti, 'usanyadire za mawa cifukwa sudziwa lidzabala ciani.' Koma cibaza munthu cidamgwira, akamba za mawa ngati moyo wake audziwa mathero. Sazindikira kuti palibe munthu amapeza mawa. Nthawi zonse mawa lisunthira mtsogolo ndipo nthawi yamtsogolo idzakhala yamtsogolo ndithu. Munthu akhoza kutembenukira ku zimene anacita ndipo nadziwa kupambana ndi kulephera kwake. Adziwa m'mene anasangalalira ndiponso m'mene anamvera cisoni tsiku lina. Tsono angakhale akuti kunkhongo kulibe maso, tikhoza kupenya zimene tinacita dzulo kapena kale tiri ana. Tikhoza kupenya ngati nchito

tinacita njopenyeka ndi maso, monga mitengo, cimanga ndi zina. Tikhoza kukumbukira, monga nkhani, ngozi ndiponso zina zambiri. Koma angakhale maso amaona kutsogolo kumene tipita, ali ndi polekezera. Athera pamene masowo angathe kufika. Kupenya kokha, koma kuzindikira cimene cingamucitikire pamene alikuyenda, sangathe kudziwa. Imeneyi ndi nthawi yamtsogolo-mawa.

Ndipo pano pali citsanzo cimene anthu ena anali kuganiza zosintha moyo wawo akakaona zinthu zotuku-la moyo wawo mawa. Dziko lina ku Ulaya, linali ndi kambali kena kosatukuka. Kadera kameneka kanazungu-liridwa ndi mapiri. Ndipo kuyenderana ndi anzawo aseri lina, kunali kubvuta cifukwa kunalibe miseu yabwino. Malimidwe awo anali acikale, olimira ndi khasu. Kuti kuli migwanda pansi (mwamuna ndine) samadziwa. Tsono popeza deralo linali la conde, magulu a m'dziko-mo oyang'anira za cakudya, anafuna njira yotukulira deralo pa za ulimi. Pa zaka zambiri anayesa kukakamiza anthu a m'deralo kuti atsate njira za makono za ulimi, powapatsa alangizi wowalangiza za kalimidwe ka makono. Koma anthu sanagwirizane nawo. Zifukwa zoletsa kugwirizana zinali izi:- Coyamba, kunali kosautsa kuwasiyitsa kalimidwe kamene anatengera kwa makolo awo. Ndipo polima mwa njira imeneyo pa nthawi yaitali, kalimidweko kanakhala ngati mwambo umene anawasiyira makolo awo. Anthu anayesa kulakwira mizimu ya makolo awo ngati ulimi woterewu saupereka kwa ana awo. Caciwiri, alangizi amene akadayenera kulangiza, anali kuuza anthu mwaukali ndi mwankhanza. Tsono cifukwa ca ici anthu sanafune kulamulidwa. Cacitatu, pokhala alangizi anali ocokera kwina, osati ana awo wobadwira m'dera lija, anali

kukaika ngati nzoona anali kuwauza. Koma zonse izi zinalephereka.

Atakanika a unduna wa malimidwe kuwaphunzitsa mowauza ndi kuwalanga, anapeza njira ina. Njira yake inali yocita citsanzo kuti iwo akaona, atengere. Anafuna kuti iwo asadziwe kuti alikuphunzitsidwa. Motero anakonza cionetsero ca ulimi m'dera lina limene linali lotukuka kale. Ndipo alimi onse a m'kadera kaja anawaitana kuti akapenye. Bvuto limene linalipo ndi lamayendedwe. A unduna wa malimidwe, podziwa kuti kulibe miseu, anawakonzera ulendo wa pandege. Anthu atamva za ulendo wa pandege, anatekeseka, ndipo nthawi zonse nkhani osacoka pakamwa ya ndege cifukwa ambiri anali asanailawe. Masiku anathamanga msanga. Ndipo anthu anali kuti mawa tilawa ndege ndiponso tikaona zosaona nkale lonse. Anthu wonse akulu, akazi ndi amuna anali zaka zaka, kukonza zobvala zabwino zoti akaonekere nazo bwino kumene apitako. Ndipo sikunatsale munthu kupatula nkhalamba, wodwala ndi ana.

Cikondwerero cinafika pa cimake pamene anamva kulira kwa ndege. Anthu anafuula kuti mawa ulendo ulipodi koma osadziwa kanthu. Usiku uja anthu onse a m'dera lija anagona cimphika wapsyerera, kugona m'tuli kukhomo. Usiku unatalika, amangoti kuce msanga; mawa libwere msanga. Nawonso a unduna wa malimidwe, poona cidwi ca anthu a m'dera losatukuka ndi cionetsero cimene anakonzera, cimwemwe cinali tsaya, kuganiza kuti zofuna zawo zikwaniritsidwa. Zoonadi, anthu mawa anali kulowa m'moyo watsopano. Kodi moyo umenewu ndiwo a unduna wa malimidwe anakhala nakakamiza anthu kuti autsate? Iai, moyo watsopano anali kuganiza sumenewu. Iwo ankaganiza zina ndipo

mwini mawa, amene mawa lonse liri m'dzanja lake anali ndi dongosolo lake la mawa.

Kutaca, anthu anali kupita ku ndege ija m'magulu-magulu; kagulu kena ka atatu ndipo mwina kena ka anthu asanu. Kuitanizana kunali kumveka, 'Bwanawe' kapena 'Make mwana, uthyola khobwe ndi m'mawa.' Wina anali kuuza mkazi wake kuti atengeretu thumba loti azikasanziramo cifukwa ndege imasanzitsa. Ndipo munthu wina anali kulawira nthumbidwa yake nailonjeza kukaigulira takudya pobwera masana. Anthu wonse analidi ndi ciyembekezo cakuti akaona zambiri zopindulitsa ndi kusintha miyoyo yawo. M'maganizo awo ankati madzulo ano tiyamba moyo watsopano. Atafika anthu wonse a m'deralo ku ndege ija, dera lonse linalibe anthu akulu msinkhu, kunatsala ana wokha wokha.

Ndege inanyamuka, ulendo wokalandira moyo watsopano kusabwera. Tsiku limenero kunacita nkhungu yoopsya, imene inacititsa mdima uja amati, mdima wokhudzika, mdima wandiwe yani? Anayatsa nyali m'ndegemo, woyendetsa ndege sanali kupenya ngakhale mpuno wandege womwe. Anayesa kuyenda mothubvula kuti athawe nkhungu, koma kunalephereka, cifukwa nkhungu inaphimba dera lalikulu m'mwamba-mo. Panthawi yaitali, anayenda m'cipundisi-pundisi, mosaonetsetsa njira kumene apita. Ndipo mosadziwika ndi modzidzimutsa ndege inagunda phiri ndipo wonse a m'ndegemo natha cipere. Wokonza cionetsero maso anali kunjira, kupenyera kuti alendo awo afika liti. Tsono patapita nthawi anamva za ngozi ija ndi kuti anthu wonse a m'dera lija atha.

Uwu ndi moyo watsopano analandira koma si moyo umene anakonzekera kuti alandire. Anasiyadi kalimidwe

ka makolo awo komanso sanatenge kalimidwe anafuna kuwapatsa. Nkhawa ya dziko lonse inali pa ana a m'dera lija. Kodi adzakhala bwanji ana wokha-wokha wopanda wamkulu? Nanga awauza bwanji za imfa ya makolo awo? Nkhani ya ana inamvetsa litsipa akulu a cionetsero cija. Ndipo anaitanirapo mitu ina kuti iwathandize kulongosola za anawa.

Anakumana anthu anzeru wocokera m'nchito zosiyana-siyana. Tsono outsa nkhani anati, nkhani yofunika msanga kuiganizira ndi yakauzidwe ka ana a m'dera lija. Awauze ndani ndipo awauze bwanji? Gulu lina linati akanene ndi a polisi, ndipo ena anatsutsa kuti ana akasweka mitima. Atatsutsana nthawi yaitali, anapeza munthu woyenera kukapereka nkhani ya cisoni ndi yoswa mtimayi, ndiye mbusa wa mpingo. Mwa mwai, m'deralo munatsala mbusa wina amene analephera kupita nawo ku cionetsero cifukwa ca ukalamba. M'mene nkhalambayo ikauzire ana, sanakhudzepo, anailekera yokha kuti iganize mafotokozedwe a imfa yotere.

Nzoonadi, anthu anatha cipere aja anakayamba moyo watsopano kusabwera ndi ana wotsala anayamba nawonso moyo watsopano. Ana asanazindikire, akulu aja anali kulongosola za kauzidwe ka ngozi ija, anafuna kulongosoleratu zina zimene sanaziganizire kuti nkucitika. Izi zinacitika cifukwa ngakhale munthu amapenya patsogolo poyenda, sapenya mtsogolo. Sadziwa akumana nciani, njoka kapena mdani wake. Ayenda m'cimutu-mutu. Maso a munthu ali kumbuyo, cifukwa adziwa zonse ndipo akumbuka pamene anakhumudwa kaya kulasidwa ndi cipanda.

Atazindikira za umasiye wa ana, ndi kuti m'mabanja ena munatsala ana osakwana zaka khumi zobadwa,

anafuna kulongosola za makhalidwe awo. Kodi anawa akhale m'nyumba za makolo awo? Nanga popeza ambiri ndi wocepa asungana bwanji? Anthu ena anaganiza zoika pamodzi ana wonse ndikudyera limodzi. Apa panali mtsutso waukuludi. Gulu lina linati ana atakhala wokha m'nyumba za makolo awo acita phukwa, komanso akawaika pamodzi aopsyedwa. Ndipo panali nsonga ina ya nkhani, anakamba za m'mene awathandizire. Awathandize bwanji? Dziko lonse lapansi likadawapatsa cuma cambiri, koma funso linali lakuti, kodi akakhala ndi zambiri sadzakhala ana aulesi? Komanso ngati awapatsa thandizo locepa, ana sadzadandaula, nayamba kuganiza za makolo anafa amene amawapatsa zosowa zawo? Nkhani yomvetsadi litsipa.

Cionetsero analephera kuonetsa nca ulimi, koma cionetsero anaciona anthu ndi cakasungidwe ka ana. Anafuna kusintha kalimidwe kamtsogolo, koma anaiwala kuti kusintha kalimidwe ndi kusinthanso miyoyo ya anthu. Mawa ulimi udzasinthika m'malo moti, mawa dera lidzakhala la cipululu ndipo miyoyo ya otsala m'deralo idzasinthika.

## KUMVETSA NKHANI

1. Chulani zinthu zingapo zimene tionera kuti munthu amaiwala za mawa?
2. Kodi munkhaniyi, mau akuti, kunkhongo kulibe maso ngoona?
3. Nkuti kunacitika nkhaniyi?
4. Bwanji sanadziwe ulimi wamakono?
5. Cifukwa ninji samagwirizana ndi alangizi a zaulimi?
6. Kodi anakonza ciani kuti aphunzire malimidwe?

7. Ngozi inacitika cifukwa ninji?
8. Kodi m'malo molandira ulimi wamakono, analandira ciani?
9. Kodi comvetsa litsipa dziko lonse cinali ciani?
10. Ncifukwa ninji anasankha mbusa wampingo kuti ndiye akafotokozere ana? Perekani zifukwa zake.

## KUPHUNZIRA CILANKHULIDWE

1. Lembani matanthauzo a mau awa:-
mdima wandiwe yani, nyama zagalu ndani, nyama ndiye fumbi, mwezi wotungira mkanda, cimunthu cosowa mphondero, ludzu lomwetsa mkodzo, wonjezerani mau ena mokha,

## CIPHIPHIRITSO

2. Mphuno salota adaombera mfiti m'manja.

## ZOKAMBIRANA

3. Mopereka zitsanzo zoyenera, kambiranani pa mitu iyi:-
(i) Mphuno salota adaombera mfiti m'manja.
(ii) Kodi nkwabwino kusungira nchito tsiku lamtsogolo?
Fotokozani ubwino wake ndi kuipa kwake.

# PHUNZIRO 8

## MAINA

Ncinthu cocititsa cidwi kupeza malo awiri a dzina limodzi. Malo ake osiyana m'makhalidwe ndi m'maonekedwe, ena atha kukhala ku cigwa ndipo ena kumapiri kapena ku nyanja. M'Malawi muli maina a malo ndi mitsinje yofanana maina. Kuli Cileka ku Blantyre ndi wina ku Lilongwe; Mtsinje wa Lingadzi ku Lilongwe, ku Dowa ndi ku Kasungu. Komanso tipeza Cikwawa kunsi kwa mtsinje wa Shire ndi wina m'mbali mwa nyanja ku Salima.

Maina awa sanangopeka anthu ai, ayenera kukhala ndi magwero ake. Pofuna kusiyanitsa, anthu amanena kuti Chileka wa ku Lilongwe kapena wa ku Blantyre. Komabe sikukwanira cifukwa safotokoza gwero lake. Tsono za Chikwawa wa ku Salima, pokamba ndi amvula zakale a ku Chigolo, anafotokoza motere:- Akuti kale azungu asanaponde phazi m'Malawi, kunalibe dzina la Chikwawa ku Salima. Dzinali anabweretsa ndi mzungu wina amene anayamba fama lake kumene akucha Chikwawa lero. Anchito ake ambiri anali Acikunda a ku Chikwawa ca ku Shire. Anthu popita kumalo kuja ankati apita ku fama la anthu a ku Chikwawa. Cina, Acikunda aja pouza anthu amati samapeza kusiyana kwa malo aja ndi kwawo cifukwa mowa amamwa kwawo unali wosasowa ku Chigolo kuja. Uwu unali mowa wa mumtengo wa mgwalangwa.

Mafumu a midzi, ali ndi maina awo wofanana pa zifukwa zingapo. Coyamba tikhoza kutenga mudzi umene unali waukulu ndi wolamulira mtunda umenewo. Mfumu imagawa anthu ena kukakhala mbali ina ndi colinga cakuti aziona zimene acita anthu wodzapempha malo m'dera lawo. Tsono mudzi uwu unatenga dzina la mudzi waukulu uja unacokamo. Cifukwa cokhala ndi dzina limodzi, mfumu yaikulu imapita m'mudzi watsopano ndi mgugu. Izi zimacitikanso ngati banja lina licokanso m'mudzi muja.

Tsono ngati mnansi wa mfumu atengapo mbumba ina nakakhala nayo kwina, pa cifukwa ca mtendere kapena udani, ngakhale amatenga dzina la mudzi uja, anthu anali kulekanitsa ndithu. Amasiyanitsa mwanjira ziwiri: Kuyambira kumanga kapena maonekedwe a mfumuyo. Ngati ndi mudzi wa Makanda, mudzi woyamba amati Makanda Catsalira ndipo watsopano amati Makanda Catuluka. Ndipo akakhala kuti afuna kupatula posonyeza maonekedwe a mfumu, mwacitsanzo ku Muomba kuli Kayembe Mkulumimba. Ici ndi cidule cakuti Kayembe wa mimba yaikulu, kapena wamkulu mimba. Pali Kayembe wina amene amayenda ndi mcira, uyu amucha Kayembe Cimcira. Ndipo maina awa akapatsa aja anakathyola bande la mudzi, wotsatira m'mbuyo amatenga dzina lomwero ngakhale alibe mimba kapena mcira.

Midzi ya alendo wocokera kutali, amacita cimodzi-modzi poipatsa maina a uko anacokera. Mwacitsanzo, Blantyre, dzina la mudzi wa ku Ulaya kumene kunacokera mzungu wodzapondera mzinda wa Blantyre m'Malawi. Ndipo midzi ya Angoni yambiri m'dziko muno, inatenga maina a ku Zululand. Nthawi zina, dzina la mudzi limakumbutsa dzina la malo ena abwino

anapenya wina ku dziko lina, ndipo mwina dzinalo kungoliwerenga m'buku cabe. M'mudzi wina, banja lina lidziwika ndi dzina lakuti Kimberley, malo amene kupezeka miyala ya daimoni kumwera kwa Afrika.

Tsono maina a anthu nawonso, amakhala ndi magwero ndi matanthauzo awo. Mwacitsanzo, mwana wa mwamuna akabadwa atamangidwa, kumwalira kaya ali m'matenda a kumbani tilowe, tate wake, amamucha Mabvuto kapena Masautso. Ndipo ngati m'banja ucembere ubvuta, kuti mwana akabadwa angopitirira, mwana wopulumuka amamucha Maliro, Kadothi, Nyamanyerere ndipo akakhala wa mwamuna amamucha Cidothi, kapena Kumanda. Maina wonsewa asonyeza madandaulo.

Maina ena atenga gwero lawo ku mcedzera. Dzinalo alipeka kucokera ku cizolowezi ca munthu. Macitidwe a munthu akhoza kukhala polumbira, podzitama kaya ndi zimene amadya mwa umbombo. Monga ena polumbira amati, pali Nyembezi, ndipo anawacha dzina lakuti ndi a Nyembezi. Ena podzitama pa ndeu anali kuti, 'Ine ndine nkhalamba ya nkhandwe yopha moduzira,' anawapatsa dzina lakuti a Nkhandwe. Ndipo wodya mbatata mwa-umbombo amachedwa Kambatata. Anthu Ena amacitira dala mwina pofuna kudzalanda dzina la munthu wina ndi cuma cake.

Izi zimacitika maka-maka pofuna ufumu wampando, kapena cuma ca munthu wopanda ana ndi anansi ake. Ndipo pang'ono-pang'ono amasemeramo mbiri ya ufumuwo pomakhudzitsa dzina lake. Akakhala wokhu-mba cuma, alimbikira kuitana dzina pamene mwini cuma akalamba kuti aziti ndi mwana wake. Maina enanso amacha modzizimbaitsa, kudzibisa kuti asamdziwe. Nthawi zambiri anthu wotere amakhala

akambere-mbere, ndi anthu wokonda kucita mbanda.

Potsiriza tikhoza kutenga gulu lina la maina limene anthu amatenga pongokondweretsedwa nawo. Mwacitsanzo, kwina kwake kunali munthu wina woyenda mokhonya, wosamba bwino ndi wodziwika ndi anthu ambiri, dzina lake Gremison Mpinganjira. Munthu wina pokhumbira dzinalo, anataya maina ake nadzicha dzina la Gremison Mpinganjira. Ndipo ana ake adziwika ndi dzina la gogo wawo ngati Mpinganjira.

## KUMVETSA NKHANI

1. Kodi dzina ndi ciani?
2. Bwanji anthu abvutika ndi kucha ana awo maina?
3. Kodi bwanji timapeza maina wofanana a malo kapena mitsinje m'dziko limodzi?
4. Bwanji mudzi umodzi utagawanika, mudzi wotuluka utenga dzina la mudzi wotsalira?
5. Pezani zifukwa zingapo zimene mafumu akuti akuti ali ndi maina amene ali nawo.
6. Kodi maina a ana amakhala ndi magwero wotani?
7. Perekani njira imodzi imene anthu acita ndi dzina pofuna kuba.
8. Kodi mafuko a anthu amasokonezeka bwanji?

## KUPHUNZIRA CILANKHULIDWE

1. (i)Pezani matanthauzo a maina awa a mugawo (a) mu gawo (b)

*Gawo (A)*

Cimkoko Msangu, Mkanthama Kacikwama, Mkanthama Kambubvu, Kalonga Sanga, Psyeda, Kalitsiro, Kamphawi, Kaliza, Kabudula, Kacola.

*Gawo (B)*

Kalonga wa ku Sanga, wosesetsa, wausiwa, wobvutika, woimba ng'oma, wodula nsonga, wobereka cola, Cimkoko wa ku Msangu, Mkanthama wa cikwama, wosasamba, Mkanthama wolumidwa ndi mbubvu.

(ii) Magwero a maina:-

(a) Mitengo yacirendo yambiri maina awo afanana ndi a zipatso zawo:

| *Cipatso* | *Mtengo* |
|---|---|
| Citsanzo: mango | mango. |
| lalanje | lalanje |
| peyala | peyala |

Pezani zitsanzo zina mokha.

(b) Mitengo ina ya momwe muno ili ndi dzina limodzi ku zipatso ndi mitengo:

| *Cipatso* | *Mtengo* |
|---|---|
| kacere | kacere |
| mpoza | mpoza |

Funani zitsanzo zina.

(c) Mitengo ya m'dziko muno, maina a mitengo amasiyana ndi a zipatso koma afanana matsinde awo:

| *Cipatso* | *Mtengo* |
|---|---|
| nthudza | mtudza |
| thowo | mtowo |
| nziru | mziru |
| maye | m'mwaye |

Funani zitsanzo zina.

(d) Mitengo ina maina a zipatso asiyana konse ndi dzina la mtengo koma afanana maina awo komalizira ndi maina a zirombo zokhala m'mitengoyo:

| *Cirombo* | *Mtengo* |
|---|---|
| bwabwa | mbwabwa |
| thondo | mtondo |
| nchiwu | mciwu |
| khuthe | mkhuthe |

Pezani zitsanzo zina.

## CIPHIPHIRITSO

2. Palibe mtsinje wopanda gwero.

## ZOKAMBIRANA

3. Ngati kungatheke yesani kupeza magwero a maina a zinthu ndi anthu.

4. Gwero la dzina langa.

## PHUNZIRO 9

### MPHATSO

Kulandira mphatso nkokondweretsa, komanso ndi koopsya. Mphatso njabwino komanso ndi yoipa. Ngakhale kuti mphatso ndi cinthu copatsidwa kapena colandiridwa kwa ulere, munthu wanzeru aliyense ayenera kukhala ndi njengunje cifukwa mphatso iriyonse iri ncolinga cake kwa wopereka. Kumbali yaopereka, ngati ndi mphatso yeni-yeni, akapereka saikumbukanso kapena kuilanguluka. Waipereka ndi mtima wonse ndipo kupatsa kotere ndiko kofunika ndi kokhumbirika. Tsono wopereka sapereka mwaciperekera ai, amatsata munthu wosowa amene mphatsoyo angaifunedi. Munthu woti mphatso ija imuthandize pausiwa wake. Mphatso iyi ndiyo imene anthu amaidziwa ndi kuidalira kwambiri. Angakhale kuli tero, palinso mphatso zina zimene tiziona munsimu.

M'midzi mumacitika mphatso zambiri zimene cifukwa ca khalidwe lake, anthu anazisandutsa ngati mwambo. Kaya cifukwa coti kupatsana pa cinansi m'mudzi womwewo. Ndipo cifukwa cina, ngati apatsa mnzake cakudya, amadyeranso limodzi. Ndi mwambo wozikika m'midzi yambiri kupatsana ndiwo wina akasowa. Mnansi wogundizana naye nyumba sangagone ndi njala cifukwa cosowa ndiwo. Mnzake amapatsako zophika kale kapena amuuza akathyoleko kumunda kwake. Nawonso amuna wina akapha ng'ombe, mbuzi

kapena nyama yaikulu yakuthengo, saleka kugawirako anzake a pamudzi. Apa ndipo paja pamatuluka mau akulu akuti, cipande catherere ciyenderana, amanena kudyerana kwa mphatso za pamudzi.

Mphatso ina ndi ya 'Konda-ine'. Mphatso ya konza kapansi kuti kam'mwamba katsike, imakhala ngati nyaiiDO yopezera mafuno abwino kwa munthu wina. Maka munthuyo akakhala waulemu, wocititsa mantha kukamba naye, poti amvane naye, amamshosha ndi mphatso ndipo akabvomera mphatsoyo, wopereka uja azika mtima kuti kudziwana kwayambika. Ndipo amadziwanadi. Ndi mtima woti azikonda iye yekha, amayamba kuulula zoipa za anzake nadzikometsa iye. Koma anthu ena amakhala kuti aonako kanthu kena kwa munthu woti ampatse mphatsoyo. Amafuna podzampemphera cinthu cina. Ndipo cifukwa ca manyazi akhoza kudzampatsa.

Ndipo ilipo mphatso ina yokakamiza ndi ciphunzitso, maka kwa ana ndi anthu amene akonda kulandira kokha, koma iwo safuna kupatsa. Mwacitsanzo, mwana sadziwa kupatsa, adziwa kulandira kokha. Tsono pofuna kumphunzitsa kupereka mphatso, pafunika cikakamizo. Ngati apita naye ku ukwati, posupa, mai amuike mphatso ija m'dzanja la mwana ndipo amuuze aponyemo yekha m'mbale muja. Ngati apereka zolima, mwana atenge yekha zolimazo napereka. Aziona kuti waperekadi. Ndipo ngati ndi wamkulu m'banja lina, tiyese kuti mwamuna ndiye kangandiwamba, mkazi wake ayenera kuyesetsa · kuphunzitsa mwamunayo kupereka mphatso. Masiku ambiri mwamuna abwera ndi nyama kapena ndiwo zompatsa anzake, koma anzake akadza kwawo acoka m'manja mopanda kanthu. Tsono mkazi wanzeru amapatsa alendo mphatso ndi mau akuti

akapatse mnzake wamkazi. Uku kukhala kubisa ugalu wa mwamuna wake, cifukwa manyazi a m'banja ndi a onse, mwamuna ndi mkazi yemwe.

Mphatso ina isonyeza ulemu, maka-maka kwa anthu a ulemu ndi mafumu. Ngati ndi mwini nyumba kaya mudzi ndiye apereka, kusonyeza cimwemwe cake polandira mlendo uja. Ndipo pamwamba pa mphatso ija pamakhala mau amalonje ndi kulandiridwa kwake ndi manja awiri. Amapatsa mphatso kusonyeza ulemu wake, osati cifukwa cosowa, kuti alibe kapena kuti sangagule ai. Mwina cimene amapatsa mlendo, iye ali nazo zambiri. Koma mlendo sakana ai, cifukwa akatero, ndiye kuti wanyoza mwini mphatso. Alandira ndi mtima wakuti nyanja sikana madzi, nthawi zonse kwake nkulandira ngakhale ibuule ndi mkhuto.

Tsono mlendo ataceza monga m'mene afunire, amapita kwawo ndipo polangiza ciyamiko ca m'mene anamsungira, amatumiza yake mphatso. Uku ndikupereka zikomo pa zimene anamcitira. Ngati satero kumakhala ngati kunyalapsya zimene anamucitira mnzake.

Mphatso ya zingwe ndiyo mphatso imene wopereka amaikapo mau ena omanga wolandira uja. Ifananapo ndi mphatso ya kondaine. Koma isiyana mwa kuti mphatso ya konda-ine ipempha pamene mphatso ya zingwe ilamulira. Mwacitsanzo pali mphatso kusukulu za lambwe *university* zimene pa Cingerezi amacha *scholarships* zimene wopereka amasankha malo wokaphunzirako ndi phunziro lake ayenera kuphunzira. Ndipo mwina amati munthuyo akamaliza maphunzirowo, akagwirire nchito wompatsa aja zaka zakuti zakuti. Citsanzo cina ncakuti, panali munthu wina wacuma amene anali ndi alongo ake atatu. Tsono pa nchito yake panali

mnyamata wina amene amamgwira pamimba pa nchito yake. Tsiku lina mnyamata uja anadandaula kwa bwana wake kuti ngati nkutheka amukongoze ndalama kuti ayambe yake nchito. Bwana anayankha kuti ndalama zoti amubwereke alibe, koma ali nayo ndi mphatso imene akhoza kumpatsa atabvomera kucita cinthu cimene ciri kumtima kwake. Mnyamata anati mumtima mwake, ndatola bomweta-mweta ndipo analankhula ndi mtima wonthunthumira, 'Pepani bwana patseni ndipo conse munene ndidzacita.' Bwana anati ampatsa K500 ndipo akwatire mlongo wake wakhwawe. Ndipo anapitirira nati ngati adzamuleka kapena kukwatira mitala adzam'bwezere ndalama zake. Mnyamata anabvomera nalandira ndalamazo nayamba nchito ndi cikwati pamodzi.

Mphatso ina ndiyopereka modzionetsera. Wopereka apatsa ndi mtima wotama, wodzikundikira ndi wodzionetsera kuti iye ndiye kanthu. Afuna ulemu cabe kwa anthu, sapereka ndi mtima wonse. Tsono panali mkulu wina amene anapatsa malaya mnzake wosauka. Wosauka uja atalandira, anathokoza kwambiri cifukwa tsopano anakhala ngati munthu pamene kale ankayenda mimba iri pamtunda. Ndipo tsiku lina malinga ncikhalidwe ca anyamata, wosauka uja anayamba kunyoza anzake kuti ndi wosauka cifukwa sangathe kubvala malaya amtengo wapatali monga ake. Ndipo mkangano uli pakati, mkulu anampatsa malaya uja anafika pomwepo naona zotumbwa za mnzake wosauka uja. Sanadziwe kuti wompatsa malaya uja wabwera. Osakhalitsa mwini malaya anamdzangamika ndi mafunso wosauka uja. Tsono analiuza gulu kuti malayawo anampatsa ndiye ndipo abvuliretu. 'Ungawaone malaya wotere iwe kaphulika, sumayenda nthiti ziri pamtunda?' anatero mkulu uja

'Bvula malaya anga.' Anthu anali pamenepo anampepesera kuti amkhululukire. Ndipo mkulu uja anapitirira kuchula maina a anthu ena amene anawapatsa zinthu zake. Ndipo manenedwe ake anali wonyang'wa.

Tsono mphatso yotsiriza, ndiyo yopereka kwa munthu wosowa. Cifundo cimakakamiza wopatsa uja kupereka ndi mtima wokondwera wosati monyinyirika. Akapereka ayesetsa kuti asaikumbukire mphatsoyo. Anthu amene anawapatsa amawaiwala ndipo safuna nthawi ina kukumbutsa za zimene anawacitira. Iyi ndiyo mphatso-mphatso ndipo ndiyo yofunika ndi yodalirika ndi anthu wonse.

## KUMVETSA NKHANI

1. Kodi mphatso nciani?
2. Bwanji mphatso yopatsana pacinansi ikhala ngati mwambo?
3. Kodi mphatso yamkomya imatani?
4. Kodi mphatso yaciphunzitso amacita maka ndani ndipo kwayani?
5. Ubwino wa mphatsoyi uli poti?
6. Nanga mphatso yacithokozo amacita ndani ndipo kwayani?
7. Pezani zitsanzo zina za mphatso ya zingwe.
8. Anthu woculuka amapereka mphatso yodzionetsera, fotokozani kuipa ndi kukoma kwake.
9. Ngati mphatso iriyonse iri ndi colinga, kodi tinganene kuti mphatso ndi cinthu caulere?

## KUPHUNZIRA CILANKHULIDWE

1. (i)Phunzirani mau awa ndipo muwagwiritse nchito mziganizo zanu;-

ugalu, monyinyirika, uthyola khobwe ndi m'mawa, outsa nkhani, phukwa, suinunkha nsima, konda-ine, munthu-munthu, katsula.

(ii)Aneni (maverebu) ena pophatikako phatikizo m'mbuyo

Mwachi – kusintha vawulo–a ndi kuikako phatikizo mtsogolo

– Ira kapena – Era, atanthauza kungocita cinthuco wopanda colinga.

Citsanzo:-

| *Phatikizo* | *Mneni* | *Mau* |
|---|---|---|
| Mwachi – | lemba | mwacilembera |
| | kamba | mwacikambira |
| | yenda | mwaciyendera. |

Ikakoni mau ena.

## CIPHIPHIRITSO

2. Mphatso ndi mbedza.

## ZOKAMBIRANA

3. (i)Anthu wolemera amapatsana mphatso, kodi mphatso zotere zigwa m'magulu woti?

(ii) Kodi mphatso ungaikane bwanji?

CIMANGIRIRO

4. Mphatso-mphatso.

## PHUNZIRO 10

### TCHOPA

Anthu ambiri akamva ng'oma za gule wa tchopa, amakumbuka gule uja amaonerera pa tsiku la cikondwerero ku bwalo la masewera la Kamuzu Stadium. Amabvinadi mosangalatsa anthu ndipo akazi ndi amuna akamazungulirana ngati nkhunda, kukhosi kwa wopenyerera kumayera kuti mbee! Gule wopanda nyimbo, gule waufulu kwa aliyense, wobvina monga afuna ndipo gule amene anthu abvala zobvala monga mwa cifuniro ca mtima wawo, maka akamabvinira kwawo. Gule uyu ndi wa mtundu wa Alomwe a ku Mulanje ndi Thyolo. Koma kwa Alomwe, si gule amene achedwa tchopa, ndi mwambo. Mwambo uwu ukhudzana ndi cipembedzo ca makolo awo. Ndipo amene aganiza zakuti tchopa ndi cipembedzo ca makolo, ndiye akhoza kweni-kweni.

Tchopa kwa Alomwe afanana ndi mfunde kwa Achewa. Makono, anyamata ndi atsikana Acilomwe acita nawo kweni-kweni cifukwa ambiri ali m'zipembedzo za cizungu. Komabe ndi cinthu cocititsa cidwi kuona Alomwe ali wonyadira kupitiriza mwambo wa mtundu wawo ngakhale panadza zipembedzo zina. Cokondweretsa ndikuti wobvina ena amakhalanso ali a khristu a mipingo yosiyana-siyana.

Monga nanena kale kuti alendo akaona Alomwe abvina amati ndiye tchopa koma osadziwa tchopa weni-weni. Kusokoneza uku kufanana ndi m'mene

anthu asokonezera matenda wochedwa 'vimbuza', opezeka ku cigawo ca kumpoto amene poona wodwala abvina, anthu amacha mabvinidwe a wodwala kuti ndi vimbuza. Kale cipembedzo cinali kucitika pa nthawi yake kamodzi kamodzi. Tchopa anali kucitika pa nthawi za mabvuto, monga kusowa kwa mvula, matenda ndi zina. Amacitika pa mabvuto wokhudza fuko ndi mtundu wonse. Mabvuto a m'banja monga mkazi akakhala wamlomo, sanali kucitirapo tchopa ai. Tsono popeza tchopa anali kukhudza wonse, malo wocitirako anali kwa kholo lalikulu la fuko. Uku kumakhala mwina kwa mfumu yayikulu m'deralo.

Macitidwe ake asiyana, kale ankacitira mwina. Pali zosintha zina. Komanso zosintha zina zimakhalapo polinganiza ndi zolinga za tchopayo. Tsono mlembi afotokoza za tchopa amene anaonerera mu caka ca 1970 m'dera la mfumu Chimaliro m'boma la Thyolo. Tchopa ameneyu anali wopempha mvula ndipo anacitika sabata loyamba la mwezi wa khumi. Ataona kuti kumwamba sikunali kuyangana mitambo kusonyeza mvula, mtsogoleri wa deralo atapangana ndi anthu, anauza akazi kusonkhanitsa makaka ofululira mowa. Mtsogoleri amatuma anyamata kumemeza m'midzi yozungulira kuti tsiku lakuti kudzakhala tchopa. Samaiwala mfumu yampando. Ndipo makono amauzanso a polisi. Masiku ano amadziwitsa a polisi cifukwa amazindikira kuti pa cimsonkhano cotere sipangalephere ndeu. Anthu ena amakhala kuti anazondana kale ndipo kopezerana amayesa malo a tchopa. Kale Alomwe anali ndi njira zawo zopewera mabvuto wotere. Anali ndi mankhwala amene amakumbira pa mphambano za njira zonse zolowa m'mudzimo. Lero agwiritsa nchito a polisi ndiponso mankhwala awo.

Mowa utapsya, ndipo kuti msonkhano uliko mawa, mtsogoleri amaloza munthu wina amene adzabindikire m'nyumba tsiku lonse kugwira mitima ya anthu. Mankhwala ena amakumbira pa mphambano iriyonse ya njira. Mankhwala awa anali wocititsa cibaza anthu wonse wobwera ku tchopa ndi mtima wa ciwembu. Pabwalo lokumana, amazikapo msasa ndipo m'kati mwake amakumbiramo ng'oma za tchopa. Kamsasa kena kopanda tsindwi, msinkhu wake kotalika kulekeza pa mcombo, anali kumanga pambali pabwalo. Mkati mwa kamsasa kaja m'makhala dzenje kuzama kwake koti kupisamo dzanja, ndebvu zikhudza pansi.

M'mawa amakaika mowa ndi ufa m'kamsasa kaja. Anthu amayamba kudza ku tchopa. Anali kudza m'timagulu-magulu ndipo ndi mabvalidwe olekana-lekana. Ena amabvala mphondo za ng'ombe, ena kupaka ufa kumaso ngati cingondo ca cinamwali ca Achewa, njiwiri, nsolokoto, madumbo ndi zina. Zina zobvinira, zina zimakhala zoopsya monga nkhwangwa, zingwanje, mipeni, ndi zina. Atafika ambiri amayambapo kubvina, codabwitsa ncakuti sayimbira nyimbo, onse abvina mwacinunu ndipo mabvinidwe a kukhosi kwake kwa aliyense wobvinayo.

Gule ali pacimake, mlembi poyenda-yenda, anakumana ndi nkhalamba ina ya dazi lamkamwa imene inamuyendetsa ndi kumuuza zina za pamalo paja. Coyamba mlembi adafunsa cifukwa ninji ng'oma anazika pansi, wosanyamula ngati ng'oma zina. Nkhalamba inayankha kuti, ng'oma za tchopa akumbira pansi cifukwa pansipo pali mankhwala odikitsa mitima ya anthu. Poyang'ana kunja mlembi anaona kamsasa, atafikapo anapenya mkati mwake munali mtsuko wa mowa ndi kacikho kopacika pampanda. Atafunsa, pomuyankha anati ndi

mowa wa azimu kuti amwe. Wina aliyense saloledwa mpaka mtsogoleri atalamula. M'dzenjemo anaikamo miyala imene anaithira ufa kufanizira mafuwa ndi ufa wogwera m'mafuwa kufanizira nsima. Nkhalamba inaloza nyumba m'mene munali munthu wogwirira mankhwala. Mankhwala anagwirirawo anali woti pa tchopa paja pasauke ndeu. Pakauka ndeu pa tchopa, panali kufa anthu woculuka cifukwa monga ndafotokoza kale m'mwambamu, wobvina anali kubvina ndi zida zoopsya.

Ndipo cifukwa coopsyedwa ndi dzina la ndeu, mlembi anacoka msanga ukana kulinda zidzale. Paja akulu adati, zengerezu adalinda kwawu kwawu ndipo pakadafunda padajiwitsa galu. Tsono patapita masiku asanu, mvula imene ankapempha inadza ndipo ici cinali ciyambi ca dzinja. Kwa Alomwe anaganiza kuti pempho lawo layankhidwa, koma kwa alendo, maganizo awo ndi wosiyana: ena akhulupirira kuti mapemphero awo analula, ndipo gulu lina likuti mvulayo inadza mwa cilasa malunji.

## KUMVETSA NKHANI

1. Kodi tchopa nciani?
2. Apezeka kuti?
3. Nanga zifukwa zocitira tchopa nziti?
4. Kodi amamukonzekera bwanji tchopa amuna, akazi ndi mfumu?
5. Tsiku litakwana, pamacitika zotani?
6. Pa tsikuli anali kuopa kwambiri zotani?
7. Nanga bvuto limeneri amalitha mwa njira ziti?
8. Fotokozani zopezeka m'kampanda ka azimu.

9. Tchopayu anacitika liti ndipo anali waciani?
10. Kodi tchopa wawo analula?

## KUPHUNZIRA CILANKHULIDWE

1. Gwiritsani nchito mau awa m'ziganizo zanu zomveka:- lula, cilasa malunji, bindikira, bindikiza maluli.

## CIPHIPHIRITSO

2. Palemberera dembo pafera nyama.

## ZOKAMBIRANA

3. (i) Kodi nsima yamakaka ndi yakandoole zisiyana bwanji?
   (ii) Nanga makolo a m'dera lanu amapempha mvula kwa Mlengi mwa njira yanji?

# PHUNZIRO 11

## NDIWO

Anthu wodya nsima, acititsa cidwi m'mene adyera. Ngakhale akuti akudya nsima, pali cinthu cina cimene cimayenda ndi nsimayo. Popanda ico anthu sangaphike nsima, agona ndi njala. Nchito yake ndi ukalambule njira ya nsima. Kuolobzya pakhosi kuti munthu ameze bwino nsimayo. Ndipo nsima ikasowa mnzakeyu, amati alikudya nsima yosipa. Komanso mnzakeyo akakhala yekha, amati alikusinkha ndiwo. Tsono kunena mwacidule tinganene kuti ndiwo ndi mankhwala a gaga.

Poyesa kufufuza kayambidwe ka madyedwe a nsima ndi ndiwo nthawi imodzi kwa amvula zakale, paoneka kuti anaiwala ambiri kayambidwe kake. Ambiri angoti anazipeza atabadwa. Anthu ayesa kuti madyedwe a zinthu ziwirizi anayambika wopanda colinga cake. Zoonadi, payenera kukhala woyambitsa ndi coyambitsa cake. Payenera kukhala munthu amene anayamba kudziwa kuti ndiwo ziolobzya pakhosi ndipo kuti pakhosi pacite mterezi kuti nsima iziterereka, pafunika cinthu cina ndizo ndiwo. Tinamva kuti makolo akalewo anali kudya nyama payokha ndiponso cimanga kapena zikhawo pazokha. Uku kunali kudya mosaphatikiza. Tsono kumapezeka kuti akadya cimanga kukhosi kumauma gwa! akadya nsima yokha imamatira pakhosi. Nazonso ndiwo pazokha, zimapweteka anthu m'mimba ndipo m'mimba mumasudzuka. Koma munthu akadya zonse, ziwirizi, amapeza bwino.

Tamva kale kuti woyambitsa ndiwo sadziwika. Koma tsopano tifuna kupeza m'mene anthu anadziwira kuti izi nindiwo ndipo izi ndi ziphe. Payenera kukhala njira zambiri za mapezedwe a ndiwo, koma pano tipereka njira zingapo zimene akuti ena anapezera kuti cakutici nkukhala ndiwo. Anthu amafuna-funa kukhala ndi moyo nthawi ya mabvuto monga njala ndi nkhondo. Munthu akazingwa, amadya ciri conse. Ndipo atsoka akadya ciphe, amafa ndipo amwai amakumika zabwino zimene ankazisandutsa ndiwo. Mapezedwe ena ndi a maloto. Pali anthu ena a mitu yoipa, oti akalota cinthu cimakhala zoona. Woterewa ndiwo anathandiza koposa kupeza ndiwo kuti mtundu upitirire. Ngati mwaiwala, takumbukani za m'Buku Lopatulika limene linena kuti, Petro atagona tulo, kumwamba kunacokera cithumba m'mene munali nyama zosiyana-siyana ndipo mau anamveka akuti aphemo nyama nadye. Ndipo mutafunsa anthu ena adzanena zawo za m'mene anapezera zakuti zakuti mwa maloto. Mapezedwe ena acitika mwatsoka kapena mwai. Mwina mosadziwika, cirombo ca mtundu wakuti cikugwa m'ndiwo zina, cipsyera limodzi nindiwozo; pakudya ndiwo adyera limodzi namva kukoma kwa mtundu wina. Poyang'anitsa m'mbale apeza mbali yina yoduka ya cirombo nacizindikira. Poyamba aopa naganiza kuti pena cirombo cija cimkomola. Masiku atapitapo ndithu, apeza akadapuma popanda pena potsina m'thupi. Tsono cirombo cotero amacisandutsa ndiwo. Masambanso ncimodzi-modzi. Comvetsa cisoni masiku ano ndi cakuti anthu analeka kupeza ndiwo zatsopano ndipo m'malo mwake atenga ndiwo za maiko ena zimene anazipeza makolo awo mvula zapita ndiponso ndiwo zimenezi sizingamere m'chire.

Tsono monga mudziwa kuti ndiwo ndi cinthu cotereza pakhosi kuti nsima ipyole bwino, cikhoza kukhala ciri conse: Zomera, nyama, zirombo kaya madzi amcere. Ndiwo nzolekana-lekana ndipo zosawerengeka. Kusiyana kumeneku kubwera cifukwa cosiyana malo, mtundu ndi khumbo. Ponena za malo tikhoza kulingirira za makhalidwe a dziko, kwa mapiri kapena ku cigwa; kogwa mvula yambiri kapena yocepa; ku nyanja kapena ku mtunda; kozizira kapena kotentha. Kuonekanso kuti mtundu ulamulira ndiwo zoyenera. Mtundu wakuti pokhala ndi ganizo lakuti umadya ndiwo zakuti zakuti zokha. Citsanzo, pali mtundu wina wa Amwenye umene sakudya camagazi ciri conse koma ndiwo zocokera ku zomera. Ndipo ndi anthu pang'ono amene sakudya ndiwo zakuti cifukwa ca khumbo.

Tsono malinga ndi zimene ndachulazi, tiona kuti mbali ya ku nyanja ndiwo zawo ndi nsomba, nkhasi, mvuwu (bokho) ndi zina za masamba. Ku mtunda ndiwo zawo ndi nyama, mbewa, nkhanu, afulu, mazira, nyemba, zirombo za m'mitengo ndi nyerere monga inswa, ndi zomera monga bowa. Ku mtunda kuli madera olekana-lekana koma ndifuna awerengi apeze wokha ndiwo zipezeka m'madera yawo. Masiku ano anthu sali kudya ndiwo zimene anapeza makolo awo cifukwa ca kalitengera, aopa kutsika. Motero nkobvuta makono kudziwa ndiwo zathu zathu nziti? Alendo anadza nindiwo zawo zimene makolo athu samazidziwa nkomwe. Mwacitsanzo, pali ndiwo zija akuti, kabici, letesi, tanapusi ndi zina.

Ndipo cifukwa ca kusiyana madera, mtundu ndi zolingirira, anthu amalimbikira mtunda wopanda madzi pomacita mitsutso yosayenera, mitsutso yonyozerana ndiwo. A ku nyanja anyoza wodya mbewa ndipo a ku

mtunda anena a· ku nyanja kuti akudya nsabwe za ng'ona. Tsono coti munthu adziwe ndico kuti, palibe ndiwo yabwino kapena yonyansa; palibe ndiwo yopambana inzake. Ngakhale ena akuti nyama kaya nsomba ndiyo yoposa, cifukwa icotsa nkhuli mkamwa. Inde, icotsadi nkhuli mkamwa, koma anthu sathera nkhokwe ndi nyama. Nyama nthawi zonse ndi mlendo m'nyumba. Anthu amathera nkhokwe ndi masamba. Cina ndico kuti anthu akudya zimene zipezeka mosabvuta m'deralo. Wokhala kouma amasunga ndiwo zawo moumika kuti nthawi ya cirimwe azikadya futsa uja. Koma wokhala kosasowa madzi saona kufunika kwa kusunga ndiwo. Kunyoza ndiwo kwina kumasonyeza umbuli, wosadziwa ndiwo nciani. Kwina kumakhala kuipidwa nazo m'maso cabe. Sakumbuka mau a akulu akuti, maso ali n'njiru koma m'kamwa mukonza. Monga mankhwala, samwera ukoma kwake koma kuti acire, ncimodzi-modzi ndiwo, adyera ndi colinga ca kufewetsa pakhosi pomeza nsima.

Kusankha ndiwo sikukhala pa mtundu pokha komanso munthu ndi munthu mnzake mu mtundu womwewo. Limakhala khumbo locitika mwa kudada kapena kuletsedwa. Polondola kuleka kwa ndiwo mwa cidada, tiona kuti anthu ena amakhala ndi munthu wina ngati citsanzo cawo. Amamuyesa wopambana pazonse ndipo ciri conse acita amati ncokhoza cifukwa wacita ngwapamwamba. Ngati sakudya ndiwo yakuti, womtsanzayo amalekanso. Koma pali kuletsedwa kweni-kweni kocitika ndi mtundu, mpingo, matenda, mankhwala umbombo ndi zina. Munthu aliyense amanyadira mtundu wake ndipo ncifukwa cake amaleka ndiwo zina zimene mtundu wake sukudya, aopa kusekedwa ndi kumcotsa m'gulu lawo. Ndipo munthu, mtundu wake ukamdulira mkuzi, kumpweteka koposa kumponya

m'kaidi. Masiku ano ena sakudya nkhumba, nsomba ya mlamba cifukwa ca mpingo. Yense wofuna mpingowo amalonjeza kuti sadzadya zimene mpingo uletsa.

Ndipo kuleka kwina kumadza ndi nthenda. Munthu akadwala nthenda yakuti, akadya ndiwo yakuti mwina atuluka zotupa thupi lonse. Akaleka kudya ndiwoyo, akhala ndi thupi labwino. Munthu wotere amaleka ndi mtima wakuti ndiwo yakuti inamuda. Koma ena amacita kuletsedwa ndi sing'anga kuti asadye ndiwo yakuti. Maka asing'anga a m'midzi ngati acitira mankhwala munthu nthawi zambiri ali ndi zoletsa zawo. Mwacitsanzo, wotemera mankhwala a mphamvu monga mangolomera ndi katukwi, amawaletsa kudya therere.

Pali anthu ena ali ndi zifukwa zawo zolekera ndiwo. Gulu lalikulu la akazi, amalekera ndiwo cifukwa ca dzimbu. Akazi woterewa amakhala kuti amuna awo alusira akagula nyama. Mtundu wina kukadza mlendo kunyumba, mkazi amaphika nkhuku yonse ndipo napatsa mlendo mphika wonse wa nyama ya nkhukuyo. Tsono akazi ambiri amaleka kudya nkhuku kukana kuti angazikhumbira nyama pophikira alendo. Amuna a ciongo ca a Moyo mwacitsanzo, sakudya mtima wa nyama iriyonse. Kutero amati adzidya. Koma nthawi zina ambiri amaleka ndiwo cifukwa cozifanizira ndi cinthu cina coipa kapena kuipidwa ndi zimene ndiwoyo ikudya. Ena sakudya nkhumba cifukwa ca zimene ikudya, osati kuipa kwa nyama yake ai. Citsanzo cina nca njobvu, ziwalo zina monga mawere ndi bweya zifanana ndi za munthu ndipo ambiri amaleka kudya cifukwa ca zimenezo. Ndipo awo m'modzi wa mtundu wawo anaphedwa ndi nyama ya mtundu wakuti wakuti, nyama ya mtundu umenewo amaileka kuisandutsa ndiwo. Koma ena cifukwa comwa mkaka wa ng'ombe,

safuna kudya nyama yake cifukwa amati ndi mai wawo wowayamwitsa. Anthu a m'midzi ena sakudya zinthu za m'zitini cifukwa comva mbiri yakuti mwina wogwira nchito yopanga ndiwo za m'zitiniwo amadulidwamo zala m'makina wogayira, maka nyama.

Tsono apa tiona kuti ndiwo ndi cinthu ciri conse cimene munthu akudya kuolobzyera mu m'mero kuti nsima ipite bwino. Kukoma m'maso kapena kuipa m'maso si kanthu koma ngati ikwaniritsa colinga cake, basi iyo n'ndiwo. Nkusowa nzeru kumene acita anthu ena amene athira malobvu akapenya ndiwo ya anzawo. Akulu amvula zakale si opusa ponena mau akuti, 'yagwa m'mbale n'ndiwo.'

## KUMVETSA NKHANI

1. Kodi ndiwo nciani?
2. Anayambitsa ndani?
3. Nanga anayamba bwanji?
4. Kodi bwanji ndiwo zisiyana-siyana pakati pa mitundu?
5. Perekani zifukwa zingapo zimene muyesa kuti ndizo zithandiza kuti pakhale ndiwo zolekana-lekana.
6. Kodi muganiza akazi analekeranji kudya ndiwo zimene iwo azikana?
7. Nanga amuna amalekeranji kudya ndiwo zakuti?
8. Kodi pali zifukwa zanji zimene anthu alekera kudya mlamba, njobvu ndi nyama ya m'citini?